


CHISINDIKIZO CHA ISITARA

 Ndithudi ndi chamwayi kukhala pano mmawa uno, pa tsiku ili la kubadwa chaputala cha Full Gospel Business Men kuno ku Phoenix, ndipo kudziwa kuti Ambuye anandipatsa ine gawo laling'ono la ilo, kuti ndidzakhale gawo la chiyanjano ichi. Ine ndikufuna ndimupatse moni M'bale Carl Williams ndi mkazi wake, M'bale Stromei, ena onse pano pa nsanja, M'bale Shores, M'bale Outlaw, atumiki, ndi nonse anthu abwino inu.

² Inu mukudziwa, ine—ine ndinali ndi tsiku lobadwa sabata yatha, nanenso. Ndipo ndine wamkulu pang'ono kuposa chaputalachi. Ndikhulupirira iye anati, “Faivi ndi...zaka zausinkhu, za chaputalachi.”

³ Winawake anati, tsiku lina, anati, “Kodi inu muli ndi zaka zingati, M'bale Branham?”

⁴ Ine ndinati “Twente sikisi.” Ndipo ine ndinati, “Ndinachotsapo zaka twente faivi zoyambirirazo. Sindinamutumikire Iye bwino bwino mu zimenezo.” Ine ndinati, “Ine ndikuyembekeza Iye adzatero, nayenso.” Kuti Iye achite izo zidzakhala zosiyana.

⁵ Koma ndi zabwino kukhala kuno. Ndipo tsopano tikufuna kuti tisatenge nthawi yanu yambiri. Chifukwa ife...ine—ine nthawizonse ndimachita mantha, nditatha kumva ena a maumboni abwino awa, ndi zinthu zimene zikuchitika, kuti ine...ndi nyimbo, kuti ine ndichita chinachake chimene chingakhumudwitse izo. Ndipo ine ndimafuna kuwonjezera kwa izo, ngati pangakhale chirichonse chimene ine ndingawonjezere kwa izo. Alongo awa...

⁶ M'bale uja amene anayimba nyimbo mmawa uno, m'bale wachikuda, ine ndinayamikira izo, *Diso Pa Mpheta*.

⁷ Ndi alongo awa amene anayimba nyimbo iyi, amene akhala amodzi a ondithandizira kuyambira pamene ine ndinali kuno nthawi yoyamba. Ine ndiri nayo iyo. Ine ndaisunga iyo pa rekodi, ndipo ndimangoisewera iyo, *Ine Ndikufuna Kudzakambirana Izo Ndi Iye*. Ndipo ine ndinamufunsa M'bale Dawson Riley kumeneko, mzanga, ngati iye angatero, ena a iwo, ngati iwo angawonetsetse kuti awatenga madona amenewo, ngati iwo akadali pano pa dziko, kuti ayimbe iyo kenanso mmawa uno. Ndipo ine ndikudalira Terry anamva zimenezo. Ndipo ine ndikuganiza iye anatero. Ine ndikufuna ndidzaichotse iyo pamene, mwinamwake, kudzaijambula kapena chinachake, chifukwa ndikuikonda kwenikweni nyimbo imeneyo. Ndipo ndiyo yanga...chokhumba changa ndi kukambirana ndi Iye. Ndikuganiza ife tonse timafuna kuchita zimenezo. Ndi chifukwa chake tiri pano mmawa uno.

⁸ Tsopano, misonkhano ikubwerayi, sabata yamawa. Kodi ndi zabwino kuti ndizitchule? [M'bale akuti, "Ndithudi."—Mkonzi]. Ine—ine ndikakhala kwathu sabata ikubwerayi, ku kachisi, Lamlungu likubwerali, ku msonkhano wa Isitara; Loweruka usiku, Lamlungu, ndi Lamlungu usiku. Ndipo kenako ine ndidzabwerera ku California. Anthu nonsenu kuzungulira ku California, ndidzakhala okondwa kukhala nanu pa msonkhano kumeneko. Ndipo ine ndikuganiza Billy watumiza kulengezetsa kolakwika. Ndi...Iye anati, "Ku Biltmore Hotel," ndikukhulupirira, "zikuyenera kukhala kumeneko." Ndi...[Wina akuti, "Analephera kuti awapeze."] Analephera kuti awapeze. Ndipo ndi ku Eastmont? ["Embassy."] Embassy, Embassy Hotel. Chotero aliyense wa anthu a Full Gospel kumeneko akakudziwitsani inu, ngati mukakhale mbali imeneyo.

⁹ Ndipo kenako ife tibwerera kuchokera kumeneko, ndipo ine ndidzapita ku South Africa kenako. Pakangotha mwezi umodzi kuchokera lero, tinyamuka ulendo wopita ku South Africa, tikuyembekezera nthawi yayikulu mwa Ambuye, pafupifupi mafuko atatu kumusi kumeneko. Chotero ife—ife ndithudi tikusowa mapemphero anu. Ine mwinamwake sindidzatha kukuwonaninso inu, ngati Ambuye apitiriza zoti tipite, mpaka ine nditadzabwereranso. Ndipo ndikuyembekeza kuti ndidzakhala ndi lipoti labwino la kwa inu tikadzabwerera.

¹⁰ Nthawi yotsiriza kumusi kumeneko, ine ndikuganiza kuti Ambuye anandipatsa ine msonkhano wopambana kwambiri umene ine ndinayamba ndakhalapo nawo. Ndipo nthawi ina, pa kuyitanira kuguwa...Tsopano, izi zinali kuchokera pa mbadwa zama bulangete. Momwe ine ndikudziwira, kunali sarte sauzande amene anamulandira Khristu pa nthawi imodzi. Ndipo ife tinkaganiza kuti mwinamwake iwo anali kutanthauza machiritso athupi, chifukwa uko kunali pafupifupi twente faivi sauzande amene anachiritsidwa pa nthawi imodzi. Ndipo tsiku lotsatira, ameya a—a Durban, amene ndi Sidney Smith, anati, "Pita pazenera lako, ukawone amene akubwera mu msewu." Ndipo apo panali galimoto yodzaza katundu pambuyo pa galimoto yodzaza katundu, zitangowunjikidwa mpaka pamwamba ndodo zakale ndi zinthu, zitangowunjikidwa pamwamba; iwowo amabwera mmbuyo, mbadwa, amene anali pa nkondo wina ndi mzake, akubwera mmisewu ya mzindawo, akuimba *Kungo Khulupirira* mu chinenero chawo.

¹¹ Ine ndikukuuzani inu, mtima wanga unakondowezeka. Monga... Pamene iwe uwona chinachake chonga icho, M'bale Shores, iwe umamverera kuti ntchito yako siinakhale pachabe ndiye. Inu mwaona, iwe wayesetsa. Ndipo ndikuyembekeza kuti Mulungu akabwerezanso zimenezo, osati chifukwa—chifukwa tikupita kumeneko, koma chifukwa chakuti tikuyembekezera Kudza kwa Ambuye.

¹² Ndipo monga nyimboyo imanenera, ife tikufunafuna yaing'onoyo, nkhusa yotayika ija, ndizo, izo...Iye—Iye sadzabwera mpaka nkhusa imeneyo italowa. Iliyonse ikuyenera kukhala mu khola. Iye sadzatseka chitseko mpaka womalizayo atalowa. Chotero, abale atumiki, ine ndiri wotsimikiza ndi inu, mmawa uno, za kuyesetsa kusaka nkhusa yotsiriza imeneyo. Iyo ikhoza kukhala mu Phoenix, mmawa uno. Ine sindikudziwa. Koma pamene yotsirizayo idzalowa, ndiye M'busa adzatseka chitseko.

¹³ [M'bale akuti, “M'bale Branham?”—Mkonzi]. Inde? [“Kodi ndinganene mawu?”] Inu ndithudi mungathe. [“Ndinaiwala chinachake. Takhala tikukamba za...” Malo opanda kanthu pa tepi.] Izo zonse nzabwino. [“Ndipo ine ndikudziwa, aliyense amaiwala chinachake, kamodzi mu nthawi.”] Ine sinditero. [“Oh!”]

¹⁴ Ndine amene ndimayenera kulemba zimene nditi ndinene, pafupifupi. Ndine...Pamene ndinayamba kukalamba, ndimapeza izo kukhala zovuta kuti ndikumbukire, kulemba Malemba anga, ndi zina zotero. Zinkakhala kuti, ine ndinkakhoza kuyala pafupifupi Malemba fifite mmalingaliro anga, ndipo sindimakhoza nkome...ndimawatchula iwo ndikamadutsa, koma ndiri ndi mailosi ovuta kwambiri kuseri kwa masiku amenewo.

¹⁵ Chotero, ife tikuyembekezera Kudza kwa Ambuye. Ambuye akudalitseni nonse!

¹⁶ Ndiyeno iwe ukafika muno, ndipo iwe umaganiza...Iwe ukakhala pansu muno ndi kuwamva anthu awa akuchitira umboni. Iwe umaganiza, “Chabwino, pamene ndikafika pamenepo, ine ndikanena chinachake chokhudza izo.” Ukatero, pamakhala zambiri zoti unene, ungakhale tsiku lonse ukunena zimenezo. Koma, ine ndithudi ndikukuthokozani inu nonse. Mulole chaputala chaching'ono ichi chipitirire kumakula. Mulole mpingo uliwonse mu Phoenix upitirire kumakula mpaka Yesu adzabwere, ndiro pemphero langa lowonamtima.

¹⁷ Tsopano, ine ndikuganiza, kuti tingozipumitsa pang'ono pokha, tiyeni tiyime pamene tikukhala ndi pemphero. Inu mutero?

¹⁸ Mulungu Wamphamvuzonse, Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, Amene munamuukitsa Iye kwa akufa, ndipo mwamupereka Iye kwa ife monga nsembe, ndi Ambuye ndi Mpulumutsi. Ife ndi oyamikira kwambiri kwa Inu chifukwa cha mwayi uwu umene ife tiri nawo mmawa uno, kudzayima mu Kukhalapo Kwanu, ndi anthu Anu amene awomboledwa ndipo akuyembekezera Kudza Kwake kwachiwiri kwaulemelo, kuti adzatilandire ife kwa Iyemwini. Ngati pali tchimo pakati pathu, Ambuye, tiyeretseni ife ndi hisope Wanu. Ndipo ife

tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu mumuchize munthu wodwala aliyense amene ali pakati pathu.

¹⁹ Ndipo ngati pangakhale, mwa mwayi, iwo amene samakudziwani Inu, mu ubatizo waukulu uwu wa Mzimu Woyera umene ife moona mtima tikulimbanirana, ndi kunena kuti izo ndi zoyenera kuchita, mogwirizana ndi Malemba a tsiku lotsiriza lino, ife tikupemphera, Mulungu, kuti Iye agwere pa ife tonse, lero, ndi kutibatiza ife mwatsopano kulowa mu Thupi, ndi kuwabweretsa iwo amene ali kunja, mkati, nawonso, Atate.

²⁰ Tidalitseni ife pamene tikuwerenga Mawu Anu ndi kuyesetsa kuti tiyankhule chimene chiri Choonadi cha Mawu Anu. Mutseke kamwa zathu ku zomwe ziri zabodza, ndipo mutsegule mitima yathu ndi kamwa zathu ku chomwe chiri Choonadi, pamene ife tikudzipereka tokha kwa Inu. Mugwiritse ntchito kamwa zathu kuti tiyankhule, ndi makutu athu kuti timve, ndi mitima yathu kuti tilandire. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Amene anadzoza izo kuti zidzakhale chomwecho. Amen.

²¹ Ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Mawu Oyera, malo atatu mu Baibulo. Ndipo ngati mungalembe izi, ndipo mukufuna kupitiriza, kuwerenga kuti mudziwe zambiri, ine ndingakhale wokondwa kwambiri ngati mungalembe izo. Malo amene nditi ndiwerenge ndi Mateyu 28:1-10, ndipo kenako Chivumbulutso 1:17-18, Aroma 8:11. Ndipo mundilole ine ndibwereze izo kenanso. Ndipo tsopano Mateyu 28:1 mpaka 10, Chivumbulutso 1:17 mpaka 18, ndi Aroma 8:11.

²² Tsopano tikuyandikira Isitara. Ndipo pamene mukupeza malo anu, ndi kulemba izo. Ine ndikuganiza kuti sabata ikubwerayi ndi sabata yopambana kwambiri ya mbiriyakale ya masabata onse a chaka. Ndikuganiza kuti chinthu chachikulu chimene tikondwerere sabata ino, sabata ikubwerayi, chinali chochitika chachikulu kwambiri chimene chinayamba chachitikapo pa dziko lapansi. Sindikuganiza kuti chirichonse chingapose izo. Inu mukuti, “Chabwino, a—kupachikidwa kunali kwakukulu.” Koma anthu ambiri afapo, amuna ambiri anapachikidwapo, ngakhale mmasiku omwewo a Ambuye wathu. Koma panali Mmodzi yekha wa iwo Amene anauka kwa akufa. Izo zinasindikiza izo.

²³ Tsopano ndikufuna kuti ndiwerenge. Ndipo uwu uli ngati uthenga waung’ono isanafike Isitara, Ambuye akalola, pafupifupi maminiti forte. Tsopano tiyeni tiwerenge kuchokera mu Uthenga wa Mateyu Woyera, mutu wa 28, kuyambira.

Pakutha kwa sabata, pamene kunayamba kucha kulowa tsiku loyamba la sabata, anadza Mariya wa Magadala ndi Mariya winayo kudzawona kumanda.

Ndipo, taonani, panali chivomezi chachikulu: pakuti mgelo wa Ambuye anatsika kuchokera Kumwamba,

ndipo anabwera, ndipo anadzagudubuza mwala pakhomo, ndipo anadzakhala pamenepo.

Maonekedwe ake anali ngati mphezi, ndipo chovala chake chinali choyera ngati chipale:

Ndipo chifukwa cha kumuopa iye anthu onjenjemera wo anachita... alondawo (mundikhululukire ine) ananthunthumira, ndipo anakhala ngati anthu akufa.

Ndipo mngelo anayankha ndipo anati kwa akaziwo, Musaope inu ayi: pakuti ndikudziwa kuti inu mukumufuna Yesu, amene anapachikidwa.

Iye sali pano: pakuti iye wauka, monga ananenera. Bwerani ndipo mudzaone malo amene Ambuye anagona.

Ndipo pitani mwamsanga, mukawauze ophunzira ake kuti iye wauka kwa akufa: ndipo, taonani, iye akupita patsogolo panu kulowa mu Galileya; kumeneko inu mukamuwona iye: taonani, ine ndakuuzani inu.

Ndipo iwo anachoka mwamsanga kumanda ndi mantha ndi chimwemwe chachikulu; ndipo anathamanga ndi kukawauza ophunzirawo.

Ndipo pamene iwo anapita kukawauza ophunzira ake, taonani, Yesu anakumana nawo iwo, akuti, Ndikuwoneni nonse. Ndipo anadza namugwira iye mapazi ake, ndipo anamulambira iye.

Kenako Yesu anati kwa iwo, Musawope: pitani mukawauze abale anga kuti apite ku Galileya, ndipo kumeneko iwo akandiwona ine.

²⁴ Ndipo Chivumbulutso, mutu wa 1, ndi ndime ya 17 ndi ya 18.

Ndipo pamene ine ndinamuwona iye, ndinagwa pamapazi ake ngati wakufa. Ndipo iye anayika dzanja lake lamanja pa ine, akuti kwa ine, Usawope; Ine ndine woyamba ndi wotsiriza:

Ine ndi iye amene ndiri wamoyo, ndipo ndinali wakufa; ndipo, taonani, Ine ndiri wamoyo kwanthawizonse, Ameni; ndipo ndiri nawo mafungulo a imfa ndi hade.

²⁵ Ndipo mu Bukhu la Aroma, mutu wa 8, ndipo kuyambira ndime ya 11.

Koma ngati Mzimu wa iye amene anamuukitsa Yesu kuchokera kwa akufa ukhala mwa inu, iye amene anamuwukitsa Khristu kwa akufa adzafulumizitsanso matupi anu achivundi ndi Mzimu wake umene ukukhala mwa inu.

²⁶ Tsopano ine ndikudalira kuti Ambuye Yesu awonjezera madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu awa. Powona kuti, Isitara, ine ndachikhazikitsa icho mu mtima mwanga kuti ndi msonkhano waukulu kwambiri, kapena chochitika chachikulu cha—chaka.

²⁷ Ine ndikufuna ndikufunsemi inu kuti mundikhululukire ine kamphindi. Kodi izo sizikusokosa kwa inu, ngati mophokosera? Kodi ziri bwino? Kodi mukuzimva zonse bwino monga choncho? Oh! Inu mukulephera kundimva. Pali bwino pamenepo, monga choncho? Sindinafuni kuti ndiyandikire kwambiri.

²⁸ Tsopano, chifukwa chimene ine ndikunenera izi, ndi chifukwa chakuti, Isitara, Iye anatsimikizira chimene Baibulo linanena. Malemba onse amene analembedwa za Iye kuti adzachita, Iye anasindikiza Umesiya Wake pamene Iye anauka kwa akufa, chisindikizo cha Isitara. Ife tiri nazo zochulukira za izo lero zimene timazikamba, zakuti, kugula zisindikizo za Isitara. Chabwino, ine ndikufuna kuti ndiyankhule mmawa uno pa: *Chisindikizo Cha Isitara*. Ndipo ndi chisindikizo chosiyana ndi chimene timagula ndi ndalama zathu, monga chisindikizo cholemba makalata, ine ndikuganiza, Tuberculosis Association kapena chirichonse chimene iwo amachitcha icho. Ine—ine ndikuganiza kuti chisindikizo ichi ndi chosiyana pang'ono. Ndipo pokhala kuti Isitara ndi tsiku lalikulu la chaka kwa ife Akhristu amene timadzitcha kuti ndife ana a Mulungu, ine ndikufuna kuti ndiyesere kulwa mu zimenezo ndi kuwona momwe ife tikuyenera kukhalira mu chiyanjano ndi chinthu chachikulu ichi chimene Khristu anatichitira ife.

²⁹ Mawu a Mulungu anayankhulidwa zambiri, zaka mahandirede ambiri Kudza Kwake kusanachitike, za kupachikidwa Kwake, ndi za imfa Yake, ndi za zowawa Zake, ndiponso za chiwukitsiro Chake. Ife tikhala tikudutsa mu misonkhano iyi, mwinamwake, sabata yamawa, pamene ife tizimvetsera ku athu—maprogramu athu apa wailesi; ndi mmatchalitchi athu, ndi azibusa athu, ndi ena otero, sabata ikubwerayi.

³⁰ Koma mwa masiku onse ndi zinthu zonse zimene Yesu anachita, ndipo ndithudi kuyamikira kutsimikizira Kwake konse kwa Mawu a Mulungu ndi zimene Iye anachita kuti awakwaniritse Iwo: za kuchiritsa odwala, kuwukitsa akufa, kutulutsa ziwanda, kulalikira Uthenga kwa osauka, ndi kukwaniritse Mawu aliwonse amene Mulungu ananena kuti Iye akanadzachita pamene Iye anabwera; ndipo kenako nkuzunzika chifukwa cha machimo athu, mmalo mwathu, kukhala chitetezero cha tchimo, pa mtanda, kumene palibe wina akanachita izo koma Iye. Koma pamwamba pa zonse za izo, ndikuganiza Isitara inasindikiza chinthu chonsecho.

³¹ Chifukwa, panakhala pali aneneri pa dziko lapansi, amene ananenera Iye asanabwere. Panakhala pali aneneri pa dziko lapansi, amene ankachiritsa odwala, ngakhale kuwukitsa akufa, ndipo ankachita zizindikiro zomwezo zimene Yesu anachita.

³² Koma Isitara inatsimikizira izo. Iyo inasindikiza Mawu a Mulungu kwanthawizonse, kwa wokhulupirira woona. Zachisoni zonse ndi kukaikira zinaphwanyidwa, pa mmawa wodala uja. Munthu anali atatsekeredwa, monga izo zinali, mu nyumba ya ndende, ngakhale kwa anthu achipembedzo lisanafike tsiku ili, chifukwa iwo anali. . . anawona kusuntha kwakukulu kwachipembedzo, ndi kusuntha kwa Mzimu Woyera, ndi zina zotero. Koma pamene munthu anafa, zinkawoneka ngati zinakhazikitsa izo. Koma pamene Uyu anadzabwera, ndipo anati, “Ndiri ndi mphamvu yoyika moyo Wanga pansu; Ndiri ndi mphamvu yowutenganso Iwo kachiwiri,” ndipo kenako nkupita kukatsimikizira chimene Iye ananena, kwa ine, icho—ndicho chisindikizo chake, pamene—pamene chinachake chinenedwa ndipo kenako nkutembenuka ndi kudzatsimikiziridwa.

³³ Ngati munthu anena, monga Columbus, ankakhulupirira kuti dziko lapansi ndi lozungulira, ndipo ankawona ngalawa, monga ife timauzidwa, momwe izo zinkabwerera, ndipo iye ankakhoza kuwuwona mlongoti asanayiwone ngalawayo. Ndipo zinamutsimikizira iye kuti dziko ndi lozungulira. Anthu sankakhulupirira zimenezo mu tsiku limenelo, koma iye anali munthu wa masomphenya. Iye anapita kuti akatsimikizire ndendende chimene iye anali nacho masomphenya, icho chinali choonadi.

³⁴ Ndipo Mulungu analingalira kuti adzatsimikizire Mawu Ake, kukhala Choonadi. Chotero Iye. . . Panali Munthu mmodzi yekha amene akanatha kuchita zimenezo, ndipo ameneyo anali Yesu. Ndipo Iye anabwera ndipo anadzatsimikizira izo kuti ndi Choonadi. Izo zinasindikiza izo. Ndipo izo zinaphwasula zisindikizo zonse za mdima, ndipo zinabalalitsa zonse—zikhulupiriro za zipembedzo zina, ndi zina zotero, kumene anthu aakulu awuka ndipo anenapo zinthu zazikulu, zodabwitsa; koma iwo ali, aliyense, ali mmanda. Koma chipembedzo chathu cha Chikhristu ndi chokhacho chimene chiri ndi manda apululu. Ndipo izo zimatsimikizira kwa ine kuti Iye ndi Mulungu wa akufa, ndi Mulungu wa amoyo, kuti Iye atha kuwukitsa akufa, nkuwabweretsa ku moyo kenanso. Ndipo ine. . . mphamvu yofulumizitsa iyi, Mzimu wofulumizitsa Wake, watsimikizira kudutsa mzaka kuti Iye ndi Mmodzi Amene angathe kufulumizitsa akufa, kubwerera ku moyo kenanso.

³⁵ Ndipo pamene Iye anatsimikizira mwa lonjezo Lake, mphamvu yogonjetsa yaikulu iyi imene Iye anali nayo, pa Isitara Iye anatsimikizira kuti Iye akanakhoza kugonjetsa imfa, gehena, ndi manda. “Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, ndipo ndiri wamoyo kenanso, ndi wamoyo kwanthawizonse; ndipo ndiri

ndi mafungulo a—a imfa, gehena, ndi manda.” Ndi ne—nenobwanji lakuti aliyense anene. Ndipo osati Iye anangonena kokha ilo, koma Iye anali atatsimikizira kale kuti Iye—Iye anali ndi chimene Iye ankadzinenera kukhala nacho.

³⁶ Ndipo ine ndikuganiza, Mulungu afulumizitse tsiku limene ife, monga Akhristu amene timakhulupirira Baibulo ili, tikhoza kudzatsimikizira chimene tikuchinena. Mukuona? Icho ndi chimene chimapanga, monga ndinanena kanthawi kapitako, “Mchere wa dziko lapansi,” mlongo anatero. Uko nkulondola. Dziko likufunafuna mchere umenewu. Ndipo pamene ife tingatsimikizire ndi miyoyo yathu, ndi mwa Baibulo, kuti miyoyo yathu ikutsimikizira Mawu amenewo kukhala amoyo lero, kuti limenelo ndi tsiku limene ife tikuliyembekezera.

³⁷ Mawu . . . “Mzimu uwu,” Aroma 8 pamenepo kuti :11 anati, “Ngati Mzimu uwu umene unawukitsa Yesu Khristu udzakhala mwa inu, udzafulumizitsanso matupi anu achivundi.” Iye sanangotsimikizira kokha kwa Iye, kwa ife, kuti Iye anali Yehova Muomboli ndipo anali ndi mphamvu pa imfa, gehena ndi manda, koma Iye watipatsanso ife mwayi wofikira kwa Mzimu womwewo, kuti ifeeni tikhoza kukhala nacho chitsimikizo kuti nafenso tafulumizitsidwa ndi Mzimu umenewo. Pakuti Mzimu umene unawukitsa Yesu kwa akufa ukamakhalama mu thupi lanu, Iwo udzafulumizitsanso thupi lanu lachivundi. Tsopano, mawu akuti *kufulumizitsa* amatanthauza “kupangidwa kukhala wamoyo pambuyo pa imfa.” Ilo litafa, kenako liyenera kufulumizitsidwa.

³⁸ Dziko latsekedwa mu kukayikira, kwa mibadwo yambiri mpaka pamenepo. Izi zinatsimikiziridwa, osati kungokambidwa, koma zinatsimikiziridwa. Ndikuganiza kuti chirichonse chimene chiri choyenera . . .

³⁹ Monga Yesu ananena, “Chifukwa chake pitani, kaphunzitseni mafuko onse; ndi kutsimikizira kwa iwo, powonetsera mphamvu ya Mulungu kwa iwo. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Iwo amene alonjeza ndi kunena kuti akhulupirira, Iye watipatsa ife kumvetsa kwathunthu kwa izo, kuti, “Zizindikiro izi zikanadzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Icho chikanadzakhala chitsimikizo cha umboni wawo. Tsopano, tikhoza kunena kuti timakhulupirira. Koma mpaka ife titakhala ndi chizindikiro chotsimikiziridwa chimene Iye ananena kuti icho chikanadzakhala pa ife, apo ayi ife *tikungovomereza* kuti ndife okhulupirira, ndipo osati okhulupirira *okhala nacho*.

⁴⁰ Pakuti, kumbukirani . . . Masiku angapo apitawo, ndimamvetsera a—programu ya pa waillesi pa KAIR uko ku Tucson. Ndipo mtumiki uyu anali atatenga mbali yolimbana ndi ife, akuti, “Chipembedzo cha chipentekoste sichinali kanthu koma chinyengo chabe. Panali . . . Nzosati uzimvetsera izo. Izo

ndi zosakhazikika.” Ndipo anati, “Munthu aliyense amene amayankhula mmalirime, ndi zinthu izi, ndi kumadzinenera kuti, amachiza odwala, ndi zina zotero, mwa pemphero, kuti ziyenera kuchoka kwa izo. Ndi kumawapempherera anthu osauka okalamba amenewo, chifukwa chakuti iwo anali mu a—kunyengedwa, kuti panali chinachake cholakwika ndi iwo.” Oh, momwe ine ndikanafunira kuti ndiyankhule ndi m’bale ameneyo kanthawi pang’ono chabe! Ndipo iye ananena kuti. . . “Izo, izo zinangoperekedwa kwa atumwi okha pa Tsiku la Pentekoste, ndipo izo zinali zonse.”

⁴¹ Ine ndikupeza kuti, zaka sarte zitadutsa, Paulo ankadzodza mphatso izi mu Mpingo. Mu Akorinto Woyamba 15, kuti, “Iye anayika mu Mpingo mphatso ya kuyankhula mmalirime, zozizwitsa. Ndipo mphatso zina zonse izi zinayikidwa mu Mpingo.”

⁴² Yesu ananena kuti. “Pitani inu ku dziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse.” Mpaka kuti? “Dziko lonse lapansi.” Kwa ndani? “Cholengedwa chirichonse.” Iwo sanaulandirebe Iwo. “Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Mpaka kuti? “Pa dziko lonse lapansi.” Kwa ndani? “Cholengedwa chirichonse. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo, mdziko lonse, ndi mwa cholengedwa chirichonse. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo: mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda; adzayankhula ndi malirime atsopano; ngati iwo adzatenga chinthu chakupha, kapena njoka, kapena kumwa chinthu chakupha, sichidzawapweteka iwo; iwo adzayika manja awo pa odwala, ndipo iwo adzachira.” Uko kunali kutuma Kwake kotsiriza kwa Mpingo, Marko mutu wa 16.

⁴³ Paulo akudzoza mphatso izi mu Mpingo, zaka sarte zitadutsa. Ndipo anati, mu Agalatiya 1:8, “Ngati Mngelo wochokera Kumwamba adzalalikira kwa inu uthenga wina uliwonse wosiyana ndi Uwu umene walandiridwa kale,” mwaona, walalikidwa kale, “akhale wotembereredwa.” Ine ndikukhulupirira kuti pentekoste inayamba popanda mathero. Ine ndikukhulupirira kuti izo zikuyenera kukhala kwa cholengedwa chirichonse, nthawi zonse, pa malo onse, kuti pentekoste izikhalapo nthawizonse. Madalitso achipentekoste akuyenera kukhala pa anthu.

⁴⁴ Ndipo tsopano, mdalitso wa chipentekoste uwu ndi chiyani? Ndi chitsimikiziro cha chiukitsiro. Nzosadabwitsa Uthenga Pawokha umatanthauza “uthenga wabwino.” Uthenga wabwino wa chiyani? Iye wauka kwa akufa. “Ndipo chifukwa Ine ndiri moyo, inunso mudzakhala moyo.” Inu amene nthawi yina munali akufa mu tchimo ndi zolakwa, Mulungu watifulumizitsa ife palimodzi, mwa Mzimu uwo umene unamuwukitsa Yesu kwa akufa. Ndipo ife tsopano tikukhala mmalo Ammwambamwamba ndi Iye, kumayanjana

ndi Iye, kumayankhulana ndi Iye. Ndi chimwemwe chotani kuwauza anthu nkhani imeneyo, amene amakhulupirira iyo kuti ndi Choonadi!

⁴⁵ Ine ndikudabwa, lero. Ndi chimene chikuchitika. Kodi ife tikuwatengeradi anthu kwa Mulungu, kapena tikungowatengera iwo ku tchalitchi? Ife tikuyenera tiziwatengera iwo kwa Khristu, kwa mphamvu yofulumizitsa iyi. Ndi chabwino kupita ku tchalitchi. Ndithudi. Ngati umo ndi motalika momwe tingapitire, sizotalika mokwanira. Pamene inu mubwera ku tchalitchi, izo ndi zabwino; koma muzipitirira mpaka kwa Khristu, mukachoka ku tchalitchiko, chifukwa ife tiyenera kulandira mphamvu yofulumizitsa iyi, ngati ife tikuyembekezera kudzhala mu chiwukitsiro chimenecho, chifukwa ndi chinthu chokhacho chimene chidzatichotse ife kwa akufa. “Pakuti ngati Mzimu uwu umene unawukitsa Yesu kwa akufa ukhala mwa inu, Iwo udzafulumizitsanso, kupanga, kubweretsa ku moyo matupi anu akufa.” Ndi lonjezo bwanji kwa ife!

⁴⁶ Tsopano zindikirani. Chofunikira kumene cha chiukitsiro ichi ndi kukanena ndi kukawonetsa, ndi kukatsimikizira kuti Yesu wauka kwa akufa. Iye sanafe. Iye ndi wamoyo. Iye akukhala moyo kuno. Iye ali mwa ife. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu. Kanthawi pang’ono ndipo dziko silimandiwonanso Ine. Komabe, inu muzidzandiwona Ine, pakuti Ine ndizidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumatsiriziro a dziko lapansi.”

⁴⁷ Tsopano, ngati Akhristu, ife tonse timadzinenera kuti Iye ndi wamoyo, kapena ife tafulumizitsidwa kuchoka—tafulumizitsidwa kuchoka ku moyo...kuchoka ku imfa tapita ku Moyo, mwa Mzimu Wake. Ndipo ngati ife sitinafulumizitsidwe, ndiye kuti sitinapangidwe kukhala amoyo.

⁴⁸ Tsopano ife tilowa mu phunziro ili, Ambuye akalola, ndi kukhala ngati tikuphunzitsa izo kwa maminiti pang’ono, momwe izo: kodi ife tafulumizitsidwa, ndipo kodi ife tikhoza kukhala otsimikiza kuti ichi ndi Choonadi?

⁴⁹ Tsopano, uwu ndi moyo wanu womwe, uwu ndi moyo wanga. Uko ndi kumene...Ngati ichi si Choonadi, chimene ndikukonzekera kuti ndinene, ndiye kuti ndine mmodzi wa anthu opusa kwambiri padziko lapansi. Ndapereka moyo wanga ku chinachake chimene palibepo kanthu, ndipo chomwechonso inu mwatero. Koma ngati icho chiri Choonadi, ndiye ine ndiri ndi ngongole kwa chirichonse chimene ine ndiri. Ndiri ndi ngongole kwa chirichonse chimene ndingakhale, kwa cholingacho, chimene ife tikuyima nacho. Ndipo ndikuganiza kuti sitikuyenera kutaya chidwi chathu.

⁵⁰ Ndipo pamene tikuwona Isitara ikuyandikira, iyo imangochita chinachake pansi mwa ine, monga ine—ine ndikudziwa kuti limenelo ndi tsiku limene chinthucho chinasindikizidwa kwanthawizonse, pamaso pa Mulungu.

⁵¹ Tsopano, ife tikuzindikira, ndi Mzimu womwewo umene unamuukitsa Iye kuchoka mmanda, umene ukukhala mwa ife. Tsopano, izo zingakhale motani? Mzimu umene unamuukitsa, Mulungu, Yesu kwa akufa, ukukhala mwa ife.

⁵² Tsopano, tsopano, ndi Mzimu umene umafulumizitsa. Si Mawu amene amafulumizitsa. Ndi Mzimu umene umafulumizitsa Mawu, kapena umapereka Moyo ku Mawu, umawapatsa Iwo mapiko kuti awuluke, kuwapatsa Iwo mwayi. Ndi Mzimu umene umachita zimenezo.

⁵³ Tsopano, tirigu, payekha, ndi tirigu basi; koma pamene moyo wofulumizitsa ulowa mwa iye, mwa tiriguyo, ndiye iwo umamupatsa iye moyo. Ndipo ife amene nthawiyina tinali akufa, opangidwa mu chifanizo cha Mulungu, ndipo komabe akufa mu tchimo ndi zolakwa, panali njira ina imene Mulungu anali nayo yoti adzatengere Moyo wofulumizitsa uwu kudzalowa mmatupi anu achivundi. Ine ndikukamba za thupi lanu.

⁵⁴ Tsopano, Yesu anali Mawu. Inu mukukhulupirira zimenezo, sichoncho inu? “Pachiyambi. . .” Yohane Woyera 1, “Pachiyambi panali Mawu, Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.”

⁵⁵ Tsopano, monga Mesiya wolonjezedwa, Iye anafulumizitsa Mawu aliwonse amene analoseredwa kuti Iye akanadzachita; kuchiritsa odwala, ndi momwe Iye akanati adzabadwire mwa namwali, zonsezo, anzipanga izo. Ndi zoon. Iye anali Mawu, akuwonetseredwa pano pa dziko lapansi, koma Iye sakanakhoza kuchita izi monga Munthu basi. Izo zinatengera Mzimu wa Mulungu, kumakhala mwa Iye, kuti ukafulumizitse malonjezo awa kwa Iye. Ine ndikuyembekeza kuti ife tikumvetsa izi momveka bwino tsopano. Yesu, pokhala Munthu, Mwiniwake, thupilo, koma zinatengera Mzimu mwa Iye, Mzimu. “Si Ine amene ndikuchita ntchitoyo. Ndi Atate Anga amene ali mwa Ine. Iye ndi Mmodzi amene akuchita ntchitoyo.” Mukuona? Yesu Iyemwini anali Mawu, chifukwa Iye anali. . .Pamaso pa Mulungu. . .

⁵⁶ Awa ndi mawu oyipa kuwagwiritsa ntchito, ndipo ndikudalira muwamvetsa bwino, pamaso pa gulu. Koma Iye anakonzedweratu mwa kudziwiratu kwa Mulungu, momwe dongosolo la Mulungu likanati lidzakhalire, kuti Iye adzatumiza Muomboli, ndipo Muomboli uyu akanakhoza kokha kudzakhala Mwana Wake Yemwe. Chotero, ndiye, limenelo linali lonjezo la Mulungu, njira yonse kuchokera mmunda wa Edeni, kuti Yesu akanadzakhala kuno. Apa Iye anali ngati Munthu, wobadwa

mwa namwali, koma zinatengera Mzimu wa Mulungu kuti ufulumizitse Mawu amenewo kwa Iye. Ndipo Iye anali Mawu, ofulumizitsidwa, Mawu ofulumizitsidwira ora limenelo. Nthawi inali itafika pamene inu munkayenera kukhala ndi Muomboli. Lamulo linali litalephera. Zinthu zina zinali zitalephera. Tsopano, zimatengera Muomboli, ndipo Iye anali Muomboli wolonjzedwa. Iye anafulumizitsidwa ndi Mawu a Mulungu.

⁵⁷ Ndipo tsopano ngati Mzimu womwewo umene unali pa Iye kuti adzakhale Muomboli mu m'badwo umenewo, umene ife tavomereza tsopano lonjezo lake mmasiku otsiriza ano, chimene chikanati chidzachitike; ngati inu mukhala gawo la Mawu amenewo, inu mwawomboledwa limodzi ndi Iye, chifukwa Mzimu womwewo umene unkakhala mwa Khristu ukukhala mwa inu, kuwufulumizitsa moyo wanu ku m'badwo uno. Ndipo Iwo nawonso, mu nthawi yotsiriza, udzafulumizitsa matupi anu achivundi, kuwaukitsa iwo, kuwabweretsanso iwo kachiwiri. Izo zimapititsa kulunda kutali pamene ife tiyang'ana pa izo. Ndipo icho—ndipo icho ndi Choonadi. Mukuona?

⁵⁸ Aroma apa, Paulo watsimikizira izo kwa ife. Mukuona? “Ngati Mzimu umene unawukitsa Yesu kwa akufa ukhala mwa inu, Iwo udzafulumizitsanso matupi anu akufa.” Uwu ndi Mzimu womwewo umene unamuukitsa Iye, umene unafulumizitsa wokhulupirira woona ku Moyo Wamuyaya. Mzimu umene unamuukitsa Yesu kwa akufa ukakhala mwa wokhulupirira, unamufulumizitsa wokhulupirira ku Moyo Wamuyaya.

⁵⁹ Ulipo Moyo umodzi wokha, Mzimu Wamuyaya umodzi, Moyo Wamuyaya umodzi, ndipo umenewo ndi Mulungu. Mulungu, yekha, ndi Wamuyaya. Ndiyeno ife, pokhala ana Ake, ndife gawo la Iye, ndizo kuti, zikhumbo za kuganiza Kwake. Ndipo ganizo likafotokozedwa ndipo limadzakhala mawu. Ndiye, munthu aliyense muno, amene ali ndi Moyo Wamuyaya uwu, analipo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, mmaganizo a Mulungu. Ndiyo njira yokhayo imene zingakhalire, chifukwa ndinu chikhumbo. Ndiko kufotokoza kwa chiganizo, kwadzasandulika Mawu; ndipo Mawu atenga Moyo, ndipo ndi Wamuyaya. Ndi chifukwa chake ife tiri nawo Moyo Wamuyaya. Mu mfundo yomweyo imene Mwana wa Mulungu wamkulu, Muwomboli; ife timadzakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, kudzera mu Mzimu womwewo, mwa kudziwiratu komweko kwa Mulungu.

⁶⁰ Tayang'anani pa mamillioni pa dziko lapansi amene sanawulandire Iwo pamene Yesu anali kuno. Koma ife tikuyenera kukhala othokoza bwanji mmawa uno, kudziwa kuti tiri ndi umboni wachindunji ndi maumboni a Baibulo, kuti ife taphatikizidwa mu mmawa waukulu wa chiukitsiro uwo umene ukubwera, Isitara yaikulu imeneyo. Ife tiri ndi chikole cha izo, pakali pano mmatupi athu achivundi. Odziwidwiratuwo

adzakhala oyambirira, ndithudi, kuti adzafulumizitsidwe, pamene Mzimu Woyera udzabwera kudzatenga Ake omwe.

⁶¹ Tsopano, pali neno lopambana, ndipo ine ndikufuna abale anga atumiki kuti ayesere kumvetsa izi. Mukuona? Pachiyambi, Mulungu, Mzimu waukulu, Iye sanali nkomwe “Mulungu” pamenepo. Iye anali Mmodzi Wamuyayayo. *Mulungu* ndi “chinthu chopembedzedwa.” Iye analibe chinthu choti chizimupembedza Iye. Kunalibeko—kunalibeko Angelo, kunalibeko kalikonse. Mulungu yekha, Iye yekha, ndi Wamuyaya. Koma, kuti akhale Mulungu, pankayenera kukhala chinachake choti chizimupembedza Iye, chotero Iye analenga Angelo, ndi Anthu, ndi Akerubi, ndi zina zotero, kuti zizimpembedza Iye. Dongosolo lake lalikulu likuyamba kufutukuka.

⁶² Koma kumbukirani, inu, mu—thunthu limene inu muli, mmawa uno, ngati inu simunali mu kuganiza Kwake pamenepo, inu simuli tsopano. Pakuti inu, pali gawo lina limene liri mwa inu, limene liri Lamuyaya, ndipo Umuyaya ndi wa Mulungu yekha. Ndipo mwa Mulungu munali kuganiza Kwake za inu mutakhala pamene inu mulipo tsopano. Mu kuganiza Kwake, ine ndinayima pa guwa mmawa uno, chifukwa Iye ndi wopandamalire ndipo amadziwa zinthu zonse. Chotero Iye akhoza kudziwa mapeto kuchokera ku chiyambi, chifukwa Iye ndi Wamuyaya. Ndipo inu, pokhala mwana wamwamuna wa Mulungu kapena mwana wamkazi wa Mulungu, ndiye inu munali mu kuganiza Kwake pachiyambi.

⁶³ Ndiyeno pamene Mzimu Woyera ubwera, ndipo inu muli pa dziko lapansi, mukuyenda kuno ngati wochimwa, pansu mmoyo wanu muli chinachake. Inu simukudziwa chimene chikuchitika, koma mukuchitira njala. Ine ndinamumva m’bale wa Chipresbateria; Ine ndinamva wa—wa Baptisti akuyankhula za, kumbuyo uko, iye anali wa—wa Freewill Baptist, akulalikira kumene iye angathe. M’bale mzanga, kuti inu, muli chinachake mwa inu, chinachake chimene inu simunachiyikemo mmenemo. Ndi chinachake chimene inu simukanakhumba kuti chidzakhale mmenemo. Ndi chinachake chotsutsana ndi chikhalidwe chanu chomwe. Ndi kudziwidwiratu kwa Mulungu, kukuchitika, Mawu a Mulungu.

⁶⁴ Monga Yesu anabadwa ali Mwana wa Mulungu, kuti adzakhale Emanuele, kuwonetseredwa kwathunthu kwa Mulungu mwa Munthu. Ndipo Iye anamupeza Iye mu kumvera kwangwiro, uko pa Mtsinje wa Yordani, akubatzidwa ndi mneneri uja. Ndipo mwamsanga pamene Iye anamumvera Iye, ndipo nkutuluka mmadziwo, Miyamba inatseguka kwa Yohane. Ndipo iye anawona Mzimu Woyera ukutsika kuchokera Kumwamba, ukuti, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa.” Mukuona? Kumvera kwangwiro, Mzimu unali utamufunafuna Iye, mu kumvera.

⁶⁵ Oh, mwamuna wosochera kapena mkazi, mmawa uno, pamene inu mwakhala pano, ndipo pali chinachake mwa inu chimene chikukuuzani inu kuti Ichi ndi choona, ndi Mzimu Woyera ukukufunani inu, kuti ukufikitseni inu ku chidziwitso cha Choonadi cha ora lino limene ife tikukhalamo tsopano, osati ora lina limene linapita, ora tsopano.

⁶⁶ Panali masauzande kumeneko amene ankamvera ora limene linadutsa. Koma kunali ora lanthawi yatsopano, limenelo linali ora limene Yesu anali woti awonekere, ndipo apo panaima Mawu. Apo panaima anthu. Ndipo apa panali mawonetseredwe a Mulungu akuchitika, kuti akatsimikizire kuti icho chinali Choonadi.

⁶⁷ Ndipo monga anthu achipentekoste, lero, ndiroleni ine ndinene ichi, kuti ife tikuyima mmasiku otsiriza ano pamene Mulungu analonjeza kuti Iye adzatsanulira Mzimu Wake pa mnofu wonse, ndipo ana Ake aamuna ndi aakazi akuyenera kunenera. Pakuti Iye anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Ndi ora lake. Ndi chimene chimapanga chirengedwe chimenecho mwa inu.

⁶⁸ Monga ine ndinayankhulira kuno, osati kale kwambiri, izo zinamveka mosinjirira pang’ono; koma ine ndikuyembekeza izo sizikutero, kwa inu, mmawa uno. Mlimi amene anayika mphungu, kapena anayika nkukhu, ndipo anali ndi dzira la mphungu. Ambiri a inu mukukumbukira nkhani ya mphungu yakale ikubereka ku—ku izi. . . Kapena, nkukhu ikubereka kuno nkukhu iyi, kapena—kapena—kapena dzira la mphungu pansa pa nthenga zake za nkukhu. Mukuona? Ndi chikhaliidwecho.

⁶⁹ Mpingo wa Presbateria, mpingo wa Methodisti, mpingo wa Baptisti, uliwonse wa iwo ukhoza kubala mphungu izi. Ndithudi. Ndi chikhaliidwe chimene chimachita izo. Monga Dr. Bosworth anakonda kunena, “Inu mukhoza kutenga dzira la nkukhu ndi kuliyika ilo pa a. . .pansi pa mwana wa galu, ndi kumangirira iye pamenepo, mwana wagalu akhoza kuswa nkukhu.” Chifukwa chiyani? Ndi chikhaliidwecho. Ndipo pamene mpingo uliwonse kapena gulu lililonse limene adzazisonkhanitse okha pamodzi, ndi kupemphera mpaka iwo kutaya tizikhulupiro tawo ndi zinthu, ndi kuyang’ana molunjika pa nkhoze ya Mulungu, iwo udzabala mphungu motsimikiza basi monga ine ndaima pano.

⁷⁰ Ndi chimene ine ndikuganiza kuti gulu la amalonda ili lachita, kuyesera kuswa chikhaliidwecho. Ife tikukhala a magulu kwambiri. Mmodzi ndi wa *ili* ndi *ilo*. Tiyeni tiswe chikhaliidwecho ndipo tikatenge chikhaliidwe cha kupembedza kwa Kumwamba. Tikonze chikhaliidwecho moyenera, mphungu zibadwa, ndipo—ndipo kuchokera mu mpingo uliwonse, kulikonse.

⁷¹ Ndipo mphungu yaing'ono iyi inayenda ndi nkuku kwa nthawi yaitali, koma ku—kulukuyo anali ngati wachirendo. Iye sankamvetsa chimene nkukuyo inkatanthauza pamene iyo inkapalasa mu—a—zinyalala za mulu wa manyowa pa—pabwalo. Ndipo icho sichinali chakudya, kwa iye. Ndipo iyo imadya tizirombo, ndi zina zotero, zimene mphungu siimadya. Chotero izo zinkawoneka zachirendo, zonse, kwa iye. Ndipo iye anali bakha wonyansa; iye anali, sindikunena izi mosinjirira, mwinamwake iye anali wa Freewill Baptist, ndipo, koma chinachake mwa dongosolo limenelo, kapena wa Presbateria.

⁷² Koma, inu mukudziwa, tsiku lina amayi ake anadziwa kuti anaikira dzira. Pankayenera kukhala mwana penapake. Chotero iye anaponyera mapiko ake aakulu mu mphepo, ndipo iye anafufuza ndi kufufuza, akufuula pamwamba pa mawu ake. Ndipo tsiku lina, iye anadutsira pa khola. Ndipo pamene mphungu yaing'ono iyi inamva kufuula kodziwika uku, iyo inali isanakumvepo iko nkale lomwe, koma iye anazindikira kuti zinamukwanira ngati golovu pa dzanja. Ndipo iye anadziwa kuti awo anali amayi ake. Iyo inadziwa kuti ameneyo anali mwana wake. Iyo inkamufunafuna iye.

⁷³ Chomwechonso Mulungu, mu m'badwo uliwonse, anawdzozeratu Mpingo Wake wa m'badwo umenewo, Uthenga wa m'badwo umenewo. Ndipo iwo akhoza kukhala ndi malamulo ndi chirichonse chimene iwo akufuna. Koma pamene ora limenelo lifika, Mzimu Woyera wa Mulungu, chimene chinali pachiyambi chinaganiziridwa ndipo chinayankhulidwira m'badwo umenewo, Mzimu umenewo umakasaka dzira limenelo. Ndipo pamene iye amva Uthenga umenewo, palibe chipembedzo cha mpingo chimene chingamugwire iye. Iye adzakwera pamwamba. Iye akuyenera kutero. Ndi mbalame yapadera. Ndi cholengedwa chapadera. Iye ndi mphungu, ndipo iye adzamva kufuulako. “Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa.”

Monga wina ananena, M'bale Williams, “Chakudya cha Nkhosa.”

⁷⁴ “Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa. Mlendo sizidzamutsatira.” Ziribe kanthu momwe mpingo wakhaira womvera, ndi kuchuluka kwa dzina lake limene iwo uli nalo. “Pamene nkhoza Zanga zidzamva Liwu Langa,” amene ali Mawu, “mlendo sizidzamutsatira.” Iwo adzapita molunjika kumene ku Mawu amenewo, ndipo akhoza kuchita izo. Ziri ngati a—a—ndi maginito.

⁷⁵ Tsiku lina, uko mu Indiana, ine ndinkayendera zigayo za zitsulo, ndipo kherere analira. Ndipo aliyense anavula ma apuloni awo, ndi kuyamba kumasesa a . . . kuchokera ku zopalira zawo, mpaka pakati pansu, zopala zimene iwo anapanga kudutsa tsikulo. Ndipo ine ndinkayenda limodzi ndi munthu amene ankandiyendetsa ine, ndipo iye anati, “Penyani ichi.” Ndipo

chotero munthu aliyense anayika chake—chovala chake chapa benchi pamwamba—pamwamba pa tebulo, nkuchokapo.

⁷⁶ Kumbuyo komwe uko, iye anakhudza kabatani kakang’ono. Ndipo apa panabwera maginito aakulu, ndipo iwo anadzatola chidutswa chirichonse cha chitsulo chimene chinapalidwa kuchokera mu zidutswa zimenezo, tsopano, ndipo chinachokapo. Icho chinazitaya izo; chinakaziponya izo mu chimbiya. Ndipo zinasungunulidwa, kukhala chidutswa china cha—cha zinthu, chinthu chomwecho, zitsulo zogwira magudumu kapena chirichonse chimene iwo ankawumba.

⁷⁷ Ndipo ine ndinayima pamenepo ndipo ndinayang’ana pa izo, mpaka ine—ndinangotaika ndekha. Ndipo ndinati, “Ndikudabwa chinachake.”

Iye anati, “Ndi chiyani icho, bwana?”

Ndipo ine ndinati, “Ndikuwona kuti zina mwa izo sizinanyamuke nawo.”

⁷⁸ Iye anati, “Ndi aluminiyamu, ndipo maginitowo samagwira aluminiyamu.”

⁷⁹ Ine ndinati, “Ndaona.” Ndipo anati. . . Kenako ine ndinati, “Chabwino, inu mukuzindikira, *apo* pali chidutswa cha chitsulo chiri pamenepo.”

“Koma, inu mwaona, bwana, icho chinamangidwa pansu.”

⁸⁰ Ine ndinati, “Ndaona.” Ndipo pamene iye anatulutsa icho, ine ndinati, “Tsopano chimachitika ndi chiyani, izo pambali *apo*?”

⁸¹ Anati, “Izo zimabwereranso ku chigayo, kudzatsanuliridwa kudutsa mchimbiya, ndipo zimabwereranso ndi kudzapanga gudumu lina.”

Ine ndinati, “Ambuye alemekezeke!” Ndi zimenezotu. Mukuona?

⁸² Pali maginito aakulu ali mu mlengalenga, amene Mulungu tsiku lina adzagwira zala Zake. Palibe munthu akudziwa nthawi imene Iye Akudza, osati ngakhale Angelo a Kumwamba, sakudziwa. Mulungu yekha akudziwa. Koma pakhala pali zodulidwapo zina zimene zachokera mu Baibulo, Akhristu a Baibulo, okhulupirira a ora lino. Mmodzi wa iwo akhoza kukhala chitsulo chogwira magudumu mmbuyo tsiku lina. *Ichi* chitha kukhala gawo lina. Zikupitirira kukapanga ulamuliro waukulu wa Mulungu. Koma izo zidzawumbidwa mu mphika wa mbiya yayikulu ya Mulungu, ndi kutsanuliridwanso kudzakhala zithunzi za Mulungu. Ndipo okhawa amene akoledwa ndi iwo adzatengedwera mmwamba. Oh, momwe. . . Ndi mwayi bwanji, kudziwa kuti pali chinachake mu chiukitsiro chimene chikukhudzana ndi ife!

⁸³ Tsopano, zindikirani, zindikirani kuitana kwa Mawu a Mulungu, kumene iye ali gawo lake. Ndipo ndi mphungu kwa mphungu. Tsopano, ngati mayi ameneyo akanafuula ngati a—mphamba, iye sakanazidziwa konse zimenezo. Iye akanangokhala basi mu kholamo. Koma kunali kufuula kwa mphungu. Munali chinachake mkati mwa kamwanako, kamene iye ankadziwa kuti iye anali mphungu.

⁸⁴ Ndipo chinthu chomwecho chiri ndi wokhulupirira woona aliyense. Pamene kulalikirira kwa Mawu a Mulungu kubwera, ndipo nkutsimikiziridwa ndi kuyesedwa kuti ndi Mawu a Mulungu a ora lino, ndiye pamakhala Chinachake mkati mwa wokhulupirira. Ine sindikusamala momwe abambo ake anali wokhulupirika ku mpingo, kapena momwe amayi ake anali wokhulupirika, kapena agogo ake, ndipo ngati mpingo umenewo ukuphunzitsa mosiyana ndi ora ili la ubatizo wa Uthenga wa Mzimu Woyera. Mumakhala chinachake mwa iye chimene chimafuula. Iye amachoka mu kholalo. Iye ayenera kuti achite zimenezo. Nkhukuyo mwina inali bwino tsiku lina, koma ili ndi ora la mphungu. Mukuona? Izo—izo ndi zosiyana. Pali chinachake, chimene, iye akuyenera kusiya khola lakalelo ndi kuwulukira kutali mmwamba. Ndiye thupi lapadziko ili limafulumizitsidwa ndi kubweretsedwa, ndi Mzimu wofulumizitsa, ku kumvera kwa Mawu a Mulungu.

⁸⁵ Tsopano, pamene Mzimu Woyera uwu, woyimiridwa ngati mphungu ikuwulukira pa dziko, ndi kumupeza wokhulupirira. “Palibe munthu angadze kwa Ine, palibe munthu angadze kwa Ine monga iye akufunira. Onse amene Atate andipatsa Ine azadza kwa Ine, koma munthu sangabwere mwa iyemwini.” Si kuganiza kwanu kwanu, kuzikokeramo nokha. Ndi Mulungu, akukokeramo. Mukuona? “Onse amene Atate andipatsa Ine azadza kwa Ine.”

⁸⁶ Tsopano, Mzimu Woyera uli pano pa dziko lapansi, ukuwafunafuna anthu amenewo amene Mulungu wawakonzera ku Moyo mu m’badwo uno. Ndipo mwamsanga pamene Iwo uwapeza iwo, Iwo umachita monga momwe Iwo unachitira pa Yesu Khristu, Mwana wamkulu wapamwamba wa Mulungu Amene anatiwombola ife tonse. Iwo umatsika ndi kudzatenga malo Ake okhalamo mmoyo wa munthu, tsopano, zindikirani, unabweretsa mphamvu yofulumizitsa. Tsopano, mphamvu yofulumizitsa ija imene inadza pa Yesu inamufulumizitsa Iye kuti adzawonetsere lonjezo lirilonse la Mawu a tsiku limenelo. Chomwechonso Mzimu Woyera umene wabwera pa ife mu tsiku lino, ngati suli mzimu woyera wachipongwe, ngati si mdierekezi kunyoza Mzimu Woyera, koma ndi weniweni, Mzimu Woyera woona. Iwo udzawonetsera lonjezo la ora lino.

⁸⁷ Pamene Iwo unagwera pa Luther, Iwo unawonetsera lonjezo lija la ora limenelo. Pamene Iwo unagwera pa Wesley, Iwo unawonetsera lonjezo la ora limenelo. Pamene Iwo ukugwa mu

tsiku lino, Iwo ukuwonetsera lonjezo la ora lino. Pamene Iwo unagwera pa Mose, Iwo unawonetsera lonjezo la ora limenelo. Unagwera pa Nowa, Iwo unawonetsera lonjezo la ora limenelo. Pamene Iwo unagwera pa Yesu, Iwo unawonetsera lonjezo la ora limenelo. Mukuona?

⁸⁸ Ndi Mzimu Woyera ukutsika pansu, kudzafulumizitsa, kudzawapanga amoyo anthu amenewo amene anadzozedweratu ndi Mulungu kuti adzakhale mu Mkwatulo. Zindikirani. Ndiko kuti, ngati iye ali mphungu yeniyeni, iye adzawumvetsa Uthenga wa ora ngati iye ali mphungu yeniyeni. Tsopano, mphungu yaing'ono mwinamwake, mu khola, inkadya bwino bwino, koma iyo—iyo inkadziwa kuti izo sizinali zolondola ndendende basi. Komano pamene iye anamva Choonadi, ndiye iye analandira Choonadi ichi. Tsopano, mu Yohane 14 . . .

⁸⁹ Yohane 5:24, kani, Yesu anati, akuyankhula mwanjira iyi, “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzafika konse ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.” Tangoganizani kuphweka kwake, “Iye amene akhulupirira.” Tsopano, njira yolondola yonenera izo, “Iye amene amvetsa.”

⁹⁰ Tsopano, inu mupite kunja kuno pa msewu ndi kukanena kwa hule uyu, “Iwe ukukhulupirira?”

“Ndithudi.”

“Iwe ukukhulupirira kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu?”

“Ndithudi.”

“Kodi unabatizidwa?”

“Ndithudi.”

⁹¹ Kupita kumusi kwa woledzera, kukati, “Iwe ukumva Zimenezo? Ukumumva mlaliki ameneyo akulalikirayo?”

“Eya.”

“Iwe ukukhulupirira Zimenezo?”

“Ndithudi.” Mukuona?

⁹² Koma, “Iye amene amvetsa, iye amene adziwa malo ake mu ora lino, iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo” (nthawi yatsopano) “Moyo Wamuyaya. Sadzabwera ku Chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Ndiye pamene Moyo Wamuyaya watsopano uwu ukhala mwa inu, Ndi chogwirizitsa, kapena chikole chakuti inu mwafulumizitsidwa kuchoka ku chivundi kupita ku chisavundi.

⁹³ Mundirole ine ndinene zimenezo kenanso. Pamene Mzimu uwu wakupezani inu, munthu panokha, ndipo wabwera pa inu, Ndi chogwirizitsa cha cholowamo chanu Chamuyaya chakuti Mulungu anaganiza za inu ndipo anakupangirani inu

asanaikidwe maziko a dziko. Chimenecho ndi chogwirizitsa chanu.

⁹⁴ Monga ngati inu mutandifunsa ine mtengo wa thundu, ndipo ine nkukupatsani inu chipatso chake. Tsopano, a—a—moyo wa mtengo wa thundu uli mu chipatso chakecho tsopano, koma inu mukuyenera kudikirira mpaka iwo udzakule.

⁹⁵ Chomwechonso ife timatero. Pamene mulandira Mzimu Woyera wa Mulungu, Ndi chodikirira chogwirizitsa cha Mulungu pa inu, chakuti wakuzindikirani kale inu. Ndipo inu munasindikizidwa ndi Mzimu wa lonjezo, wa Mulungu, kulowa mu Thupi la Khristu. Pamene Mulungu anayang'ana pansi pa Kalvare ndi kumuwona Yesu akufa, Iye sikuti anangoti. . . Iye anafera Mkwatibwi Wake, Thupi, limene liri Mpingo wa Mawu, Mpingo umene umakhulupirira Mawu a Mulungu a m'badwowo, kaya ndi mapazi, thupi, mutu, kapena chirichonse chimene chiri. Mukuona? Ndi. . . Khristu anali akuwukha magazi ndi kufa. Ndipo Mulungu, poyang'ana pa Iye, anawona chiukitsiro Chake, ndipo Mpingo unauka ndi Iye pa Isitara.

⁹⁶ Tsopano, ndikufuna kuti muzitenge zonsezi pamodzi, chifukwa ine ndiri ndi chinachake apa pang'ono pokha, ine ndikufuna kuti ndinene, Ambuye akalola.

⁹⁷ Tsopano zindikirani. Ndi chikole, kapena chogwirizitsa. Mphamvu yofulumizitsa ya chiukitsiro chanu, pamene inu mulandira Mzimu Woyera, zikatero ndiye kuti ukukhala mwa inu, kugwirizitsa kwakeko.

⁹⁸ Zindikirani, inu—inu tsopano muli paulendo wanu, mukukula kufikira ku chiukitsiro chathunthu. Palibe mtengo umene umangokula usiku umodzi. Iwo ukuyenera kukula, pamene ife tikukula mu chisomo ndi chidziwitso cha Mulungu. Inu mumabatizidwa kulowa mu Mzimu Woyera. Tsopano, pamene Mpingo wa chipentekoste, ubatizidwa kulowa mu Mzimu Woyera, Iwo wayamba kukula. Nthambi zafa. Iwo ankazidula izo. Koma Mtengowo ukukulabe, ukupitirirabe, chifukwa Iwo ukuyenera kubwera ku chiukitsiro.

⁹⁹ Iwo amatsogozedwa ndi Mzimu, kuti afulumizitse Mawu kwa inu amene muli okhulupirira. Mawu amapitirira kumafulumizitsa, pamene inu mufika ku nthambi yoyamba, nthambi yachiwiri, nthambi yachitatu, kupitirira chokwera. Iwo amangopitirira kufulumizitsa. Mzimu wa Mulungu umapitirira kumafulumizitsa kwa inu.

¹⁰⁰ Zindikirani kuti, Pentekosite, matupi awo anafulumizitsidwa ndi Moyo watsopano umene iwo anawulandira. Izo zimandipangitsa ine kumverera mwachipembedzo. Taganizani. Tsopano, apa panali amuna, asodzi, okhometsa msonkho, akazi aang'ono odzichepetsa a. . . ndipo amayi apanyumba awamba, anamwali achitsikana aang'ono. Iwo anali okhulupirira. Iwo ankakhulupirira kuti

ichi chinali Choonadi. Iwo ankakhulupirira kuti, pamene Yesu anafa (Iwo anakhulupirira pa Iye.) ndipo anawuka kachiwiri, kwa akufa, iwo ankakhulupirira kuti uwo unali mwamtheradi umboni wa Mulungu, kuti Iye anali atamufulumizitsa Iye ku moyo.

¹⁰¹ Tsopano, iwo anapita mmwamba, ku Tsiku la Pentekoste, kuti akalandire mtheradi wawo. Kodi mumadziwa chimene mtheradi uli? Ndi pamene chikalata chaumwini chakonzedwa. Iwo anapita kumeneko kuti akalandire mtheradi wawo. Ndipo anafulumizitsidwa, kapena ndi chokondoweza bwanji! Iwo anali atagula dzikolo; linagulidwira iwo. Iwo anali atalilandira ilo.

¹⁰² Kodi izo nzoona kapena ayi? “Ife tinamuwona Iye akuuka, koma tsopano nanga bwanji ife? Ndife mboni. Ife tinayima ndipo tinamuwona Munthuyo akupachikidwa. Ife tinawona mitambo ikubwera padziko lapansi ndi kudzadetsa mmwamba. Ndipo a—dziko linapanga phokoso ndi kugwedezeka; ilo linali ndi kugona modzilambatitsa kwamanjenje. Ndiye pamene. . . Iwo anamuika Iye mmanda. Iwo anamulasa Iye mu mtima, ndi nkondo, ndipo anatsitsira thupi Lake pansu ndi kudzaliyika ilo mmanda a Yosefe Arimateya.”

¹⁰³ Ndipo kenako iwo anadzapeza, kuti, pa tsiku lachitatu, Iye anauka kachiwiri. Ndipo monga wophunzira ananenera, “Ife ndi mboni za izi. Ife tinamuwona Iye akuuka. Ife tikudziwa kuti Iye ali moyo.”

¹⁰⁴ Tsopano kodi zimenezo zinachita chiyani? Izo zinachotsa mantha onse. Nzosadabwitsa Yesu anati, “Musaope ayi. Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, ndipo ndiri wamoyo kwanthawizonse.” Mukuona? Izo zinachotsa mantha onse, pamene iwo anachita izo.

¹⁰⁵ Tsopano, koma pamene iwo anapita ku Pentekoste, pamenepo iwo analandira mphamvu yofulumizitsa, mphamvu imene inawapangitsa iwo kukhala amoyo.

¹⁰⁶ Tsopano pamenepo ndi pamene ine ndikuganiza kuti, inu abale Achipresbateria ndi Amethodisti, inu mumalandira mogwirizitsa pa kukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, koma mtheradi sunabwerebe. Kumeneko ndi kukonzekera kwa chikalata cha umwinicho.

¹⁰⁷ Mulungu anamupatsa Abrahamu lonjezo. Abrahamu anamukhulupirira Mulungu, ndipo kunawerengedwa kwa iye chirungamo. Koma Iye anasindikiza pangano ndi chisindikizo cha mdulidwe.

¹⁰⁸ Ndipo Mulungu amakupatsa iwe lonjezo, mokugwirizitsa, kuti iwe udzalandira ilo, ndipo inu mudzaukitsidwa, thupi ili lidzakhala ndi ulemelero ndi Iye pa nthawi yotsiriza. Koma, inu mwaona, inu muyenera kupeza chilolezo pa chikalata chaumwini chimenecho. Ndipo chilolezocho ndi pamene chirichonse chotsutsa icho chachotsedwapo, ndipo inu muli

nawo mtheradi wa icho. Inu muli nacho chisindikizo. Ndi chanu. Chirichonse chiri pamenepo ndi chanu. Amen.

¹⁰⁹ Ndipo pamene ife tikhulupirira pa Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wathu, ndi kulapa ndi kubatizidwa, ndi kubwera kudzamukhulupirira Iye; Mulungu amazindikira kulapa kwathu ndi chikhulupiriro chathu kwa Iye, ndipo amatumiza pansi mtheradiwo. Ndipo mtheradi ndi chitsimikizo. Ndi umboni kuti, chirichonse chimene chinaikidwa mokutsutsani inu, inu munalapa bwino bwino. Aleluya! Ndipo katunduyo wagulidwa, ndipo inu mukugwirizira mtheradi wa chitsimikizo.

¹¹⁰ Winawake ayerekeze kukuchotsani inu pa malopo, kunena kuti iye ndi ake, ndipo inu muli ndi mtheradi mdzanja lanu. Muloleni iye ayesere kuchita izo. Mulibemo lamulo mdziko limene lingachite izo, chifukwa inu mukugwirizira mtheradi.

¹¹¹ Ndipo palibe mdierekezi, palibe mpingo, kapena fioloje iliyonse, imene ingadutse malire a kutsimikizira kwa Mulungu ndi mtheradi, kuti ubatizo wa Mzimu Woyera watizindikira ife mwa Yesu Khristu. Ndife otsimikiza basi kuti tidzawuka monga Iye anauka, chifukwa mogwirizitsa ife tinawuka kale mwa Iye. Amen.

¹¹² Zinthu zakale. Kodi izo zimachita chiyani ku matupi athu achivundi? Izo zimatembenuza kuganiza kwathu, zimasintha zikhulupiriro zathu. Zimayika zokonda zathu pa zinthu zimene ziri Kumwamba. Ndipo kusuta, kumwa, njuga, zinthu zimene inu munkachita, ndi zakufa. Ziri pansi panu.

¹¹³ Ndipo inu mwafulumizitsidwa. Ndipo mphamvu yofulumizitsa iyi imabweretsa thupi lanu mu chikhaliidwe chokwatulidwa, pomwepo. Zindikirani anthu achipentekoste kumtunda uko, pamene iwo anafulumizitsidwa ndi Mzimu Woyera. Mvetserani kwa ine. Pamene gulu la chipentekoste lija kumtunda uko, pa Tsiku la Pentekoste, linalandira mtheradi wa chikalata chaumwini chawo kuchokera kwa Mulungu, ndithudi, izo zinalemekeza miyoyo yawo. Iwo anafuula. Anawona malirime a Moto akugawanika pa aliyense wa iwo. Ndipo izo zinafulumizitsa matupi awo, mpaka iwo samatha kuyankhula mu chinenero chapa dziko konse. Izo zinafulumizitsa matupi awo ku chinenero Chakumwamba, Malo amene iwo akupitako. Mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu inagwedezwa matupi awo akufa chomwecho, mpaka chinenero chawo chonse cha chivundi chinasinthika, kusandulika kukhala chinenero cha chisavundi. Ndi mphamvu yofulumizitsa bwanji! Chiyani? Chinachake chimene chiri chanu.

¹¹⁴ “Ngati Mzimu umene unawukitsa Yesu kwa akufa, ukhala mmatupi anu akufa, Iwo udzafulumizitsanso matupi anu achivundi.” Ife timafulumizitsidwa ndiye ndi mphamvu ya Mulungu wamoyo.

¹¹⁵ Malirime, anafulumizitsidwa ku chinenero chatsopano cha Kumwamba, kuti aziyankhula kwa iwo; kukwatulidwira mmwamba, kuwukira kupita mu chikhalidwe chosiyanasiyana kuposa chimene iwo anayamba akhalamo. Ndiponso, ndi Moyo wofulumizitsa watsopano kwa iwo, umene unabwera mwa iwo, Iwo unafulumizitsa chinenero chawo. Iwo anayankhula mmalirime atsopano. Oh, inde!

¹¹⁶ Tsopano awoneni iwo. Iyonso inakonzedwa kuti iwapatse iwo, pambuyo pa mtheradi uwu, iyo inapangidwa kuti iwapatse iwo lonjezo lililonse limene linali pansi. Lonjezo lililonse pa maziko a Mawu a Mulungu, limene linalonjezedwa mu Baibulo, mphamvu yofulumizitsayo inaperekedwa kwa iwo, kuti ikafulumizitsire lonjezo limenelo kwa iwo. Chotero, iwo anaika manja awo pa odwala, iwo anachiritsidwa. Iwo anayankhula mmalirime atsopano. Iwo anachita zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa, chifukwa izo zinali mu lonjezo la Mulungu. Ndipo pamene Yesu anafa, kuti adzawombolenso izo kubwerera kwa iwo, malo amene anali a ana a Mulungu, Iye anawonetsera chimene Mulungu anali.

¹¹⁷ Kodi tingayerekeze bwanji kuyanjana ndi izi ndi kuziyika mu bungwe? Ife tiribe ufulu wochita zimenezo.

¹¹⁸ Ndi Mzimu Woyera, lero, ukusakasaka mitima yoona imene idzakhulupirire Uthenga umenewo. Chirichonse mu Baibulo, chimene chinalonjezedwa, ndi cha kwa wokhulupirira ameneyo. Ndipo pamene inu muvomereza izo mu chidzalo chake, ndipo Mulungu nkudziwa kuti inu muchita izo, Iye amakupatsani inu mtheradi kwa izo. Ndipo zikatero lonjezo lililonse limene linapangidwa limakhala mwa inu, ndipo Mzimu Woyera umakhala pamenepo kuti ufulumizitse izo kwa inu. Oh, mai! Kodi—kodi ife tikuyenera kukhala anthu otani? Nzodabwitsa bwanji kuwuwona Mzimu Woyera waukulu wa Mulungu pano ukuchita mphamvu imeneyo! Taganizani za zimenezo. Pamene, Mzimu Woyera Iwowokha, pano kuti uchitire umboni za ora lino. Yesu ananena chomwecho. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

Munthu aliyense angayerekeze bwanji kufufuta zimenezo kuchokera Uko?

¹¹⁹ “Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita,” Yohane 14:12. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Chimenecho ndi chitsimikizo. Pamene ife tiwona gulu la anthu litakhala pamodzi, ndipo zizindikiro zimenezo zikudziwonetsera zokha, ndicho chitsimikizo kuti mtheradi ulipo kuti uwonetsere kuti icho ndi chuma cha Mulungu. Amen.

¹²⁰ Chotero, ife ndi Isitara, nafenso. Amen. Ife tsopano tiri mu Isitara yathu. Ife tinauka kale, aleluya, kuchokera ku zinthu za mdziko, kupita ku zinthu za lonjezo la Mulungu. Osati tidzatero; ife tatero. Ndi zogwirizitsa.

¹²¹ Ndi lonjezo la Mulungu. Iye akanadzatsanulira Mzimu Wake mmasiku otsiriza, ndipo ndicho chimene iwo akanati adzachite. Zindikirani, anaika manja awo pa odwala; chirichonse chimene chinali mu lonjezo la Mulungu. “Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga mmasiku otsiriza, pa mnofu wonse. Amuna anu akale adzalota maloto. Anyamata anu adzawona masomphenya.” Ndipo malonjezo onse osiyanasiyana awa amene Iye anawapanga, chirichonse chiri mmenemo mu lonjezo la Mulungu. Yesu anawombola izo kwa ife. Ndipo pamene ife tikhala . . .

¹²² Kapena, ife, ngati tinadzozedwera pa malo amenewo, ngati ife tinadzozedwa kuti tidzakhala pa malo amenewo; monga mphungu ikuyenda mu chisa cha nkukhu. Ngati inu munadzozedwera pa malo amenewo, Mzimu Woyera uli pano kuti ukupezeni inu. Ndipo pamene Iwo ukupezani inu, inu mudzazindikira kuitana Kwake. Inu mudzalidziwa ora limene mukukhalamo. Inu mumadziwa kuti zinthu izi zikuyenera kuchitika. Mwamsanga inu mumakwatulidwa kuti mukakomane ndi Iwo, ndipo tsopano inu mwakhala mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu. Oh, ndi lonjezo bwanji! Ndi Atate Akumwamba otani, Amene angatipatse ife zinthu izi!

¹²³ Mzimu umafulumizitsa chiyanjano chawo ndi Mulungu, kuti akaitanire akufa ku moyo, mu tsiku limenelo. Iwo ankaika matupi awo pa akufa; iwo amakhala ndi moyo. Mvetserani mwacheru. Iwo ankachita zinthu zomwezo zimene Yesu ankachita chifukwa Mzimu womwewo, umene unali pa Iye, unali pa iwo. Ngati Mzimu umodzi umampangitsa munthu kuchita mwanjira iyi, iwo umpangitsa winayo kuchita mwanjira imeneyo. Ngati mmodzi . . .

¹²⁴ Kodi Izi zingatheke bwanji, kunena kuti iye ali ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo nkumakana ntchito za Mulungu? Sangachite zimenezo.

¹²⁵ Zindikirani. Moyo wa Mulungu, umene mu Chigriki umatchedwa *Zoe*, ukuyenderera kuwadutsa iwo ndi mwa iwo, unafulumizitsa malingaliro awo ku Mawu Ake. Tsopano, ndiloleni ine ndinene izo mwakachetechete kwenikweni tsopano. Mzimu wa Mulungu umene umayenda pakati pa anthu, umafulumizitsira malingaliro a munthuyo ku lonjezo la Mulungu. Mukuona? Izo zimachita izo. Taonani. Ndipo ndikuyesetsa kuti ndikuwonetseni inu a—a . . . ndi kukulolani inu kuzindikira kuti ine ndikuyankhula tsopano za Mpingo, ndiponso unafulumizitsidwa ku Moyo, mwa Iye.

¹²⁶ Ngakhale, iwo anali kokha zikhumbo Zake, kuyamba ndi kuyamba. Koma ngati Mulungu anati, “Mu tsiku *lino*,” mmbuyo pa chiyambi, “John Doe adzakhala mtumiki Wanga,” zaka mamillioni zapitazo. Tsopano, John Doe anabawira mu

tchimo, anawumbidwa mu kusaeruzika, anabwera pa dziko akuyankhula mabodza, chifukwa iye ndi wachivundi. Koma, mwinamwake, iye adzakhala ndi kumverera kwachipembedzo pang'ono. Iye adzajowina mpingo. Mwinamwake iye adzajowina mpingo wa Chipentekoste. Sindikudziwa. Iye akhoza kujowina chirichonse. Koma muloleni iye adzakhale pansu pa chikhaliidwe cha Mulungu, kamodzi. Mukuona? John Doe akuyenera kuzindikira Yemwe Atate ake ali, chimodzimidzi munga momwe mphungu ija inazindikirira chimene mayiyo anali. Iyo ikuyenera kuzindikira izo. Mukuona? Kokha, kuti John Doe ndi chikhumbo cha Mulungu chimene chasandulika mawu, oyankhulidwa, ndipo zikatero Mzimu Woyera umafunafuna mawu amenewo. Ndi izi apa. Iye amamuitana iye, amamupatsa iye Moyo wosatha, ndipo amamubweretsa iye mu Kukhalapo kwa Mulungu, Mawu a Mulungu.

¹²⁷ Taonani. Mulungu anali nacho chomwecho pamene Iye anamuwona Yesu. Iyo inali—inali ntchito yomalizidwa imene Mulungu anaimaliza ndi Yesu, pamene Iye anati, “Kwatha.” Madongosolo onse anatsirizika.

¹²⁸ Ndipo pamene Mzimu wa Mulungu ufika pa inu, ndipo inu ndithudi ndi chimodzi mwa zikhumbo za Mulungu zimene Iye anazinena. Tsopano, ngati inu simuli, inu muzidzakhala mukudabwa ndi kusokonezeka, ndi kuthamangira *apa* ndi *apo*, ndi china chirichonse, ndipo osafika konse ku chidziwitso cha Choonadi. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Ngati inu muli mmodzi wa iwo, zinthu zakale zimachoka mwamsanga ndithu, mwaona, ndipo inu mumadzakhala watsopano, ndipo dongosolo la chipulumutso limatsirizika. Inu mumakhala okonzeka kumvera Mawu aliwonse amene Mulungu anayamba wayankhulapo za inu, mwaona, kuti inu muzichita. Inu mumakhala ogonjera ku Mawu Ake. Mgwirizano, ndendende, mtheradi ku mgwirizano, chikalata cha umwini ndi chanu. Ngongole zonse zalipidwa. Izo zonse zachotsedwapo, ndipo munga zinakhalira pa Tsiku la Pentekoste.

¹²⁹ Tsopano tiyeni ife tizindikire kufulumizitsa, Mzimu wofulumizitsa uwu pa anthu ena.

¹³⁰ Tsopano, ine ndinakuuzani inu kuti ine sindiyankhula motalika kwambiri, ndipo ine ndangotsala ndi maminiti twente kuti ndikwaniritse mawu anga, ngati ndingachite zimenezo, zindikirani, kuti ndikhalebe mu nthawi imene ine ndinanena, pafupifupi—pafupifupi ora.

Zindikirani tsopano mphamvu yofulumizitsa iyi. Imene imangobwera. . .

¹³¹ Tsopano, pali zonyoza zambiri za Iyo. Pali anthu ambiri amene amaganiza kwenikweni kuti ali ndi Iyo, pamene iwo alibe. Anthu ambiri amachita izo chifukwa ali ndi malingaliro abodza ena pa chimene anawona Akhristu ena akuchita.

Satana akhoza kutsanzira chirichonse cha izo. Ife tikudziwa zimenezo. Ndipo monga amishonare, inu mukhoza kuwona izo zikutsanziridwa: kufuula, kuvina, kuyankhula mmalirime, zinthu zonsezi. Inu mukhoza kuziwona izo zikutsanziridwa paliponse. Mwamtheradi. Pakati pa achikunja ndi anthu amene amakana kuti kuli chinthu chonga Yesu Khristu kukhala Mwana wa Mulungu. Mukuona? Ndipo iwo amachita zinthu zonsezo, iwoeni.

¹³² Koma weniweni, Mzimu wofulumizitsa woona umene umabwera kwa wokhulupirira, umamufulumizitsa iye ku Mawu a Mulungu, ndiko kubwerera ku Chakudya cha mphungu kachiwiri, kubwerera kumene iyo imakhala. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.”

¹³³ Tiyeni tsopano tizindikire Mzimu wofulumizitsa uwu pamene Iwo ubwera pa anthu ena, monga Iwo unachitira pa—pa Tsiku la Pentekoste.

¹³⁴ Tiyeni tizindikire Pentekoste, momwe iwo anachitira, ndipo tiwone ngati iwo anafulumizitsidwa ndi mphamvu yofulumizitsa iyi imene ife tikuyikamba. Pa Tsiku la Pentekoste, iwo onse ankayembekezera kumtunda uko. Mwa iwoeni, iwo anali ndi mantha. Ayuda, basi zimene akanati achite, chotero iwo ankachita mantha. Koma chinachitika ndi chiyani? Pamene mphamvu yofulumizitsa iyi inagwa kuchokera Kumwamba, apo panali kulimba mtima kunayikidwa pa iwo. Panali chinachake, kumvetsetsa, kumene iwo sanali otsimikiza kwambiri za izo maora angapo mmbuyomo. Iwo ankadziwa kuti Iye anali—Iye anali atamwalira.

¹³⁵ Iwo ankadziwa kuti Iye anali atauka. Iwo anali atayankhulana Naye panjira. “Koma kodi chinthu chimenecho chinali cha iwo, kapena zinali za iwo okha, kwa Yesu Mwiniwake?”

¹³⁶ Koma apa pa Tsiku la Pentekoste, Mzimu Woyera, mtheradi unagwa pa okhulupirira. Izo zinawapanga iwo gawo la chiukitsiro Chake, zinamupanga iye gawo la chiyanjano Chake. Mzimu Woyera unadza ndipo unadzatsimikizira kwa iwo kuti adzaukitsidwa, chifukwa mogwirizitsa iwo anali ataukitsidwa pamenepo, kuchokera ku amantha kukhala amuna olimba mtima.

¹³⁷ Iwo anali—iwo ankawopa Mawu omwewo amene iwo anali atawaganizira. Musalole izi zikudutseni inu. Iwo ankachita mantha. Iwo ankadziwa kuti Iye anali Mawu amenewo.

¹³⁸ Ngakhale Ayuda anavomereza zimenezo. Nikodemo anati, “Rabbi, ife tikudziwa kuti Inu ndi mphunzitsi wochokera kwa Mulungu. Palibe munthu angachite zinthu zimene inu mukuchita kupatula Mulungu akukhala ndi Iye. Tsopano, ife tikudziwa izo. Ife tikuzindikira zimenezo.”

139 Chotero ophunzira . . . Petro anali atalumbira Pamaso Pake. Onse a iwo anali atamusiya Iye pa kupachikidwa.

140 Koma apa iwo ali tsopano mu chipinda chapamwamba ichi, mu Kukhalapo kwa Mulungu. Kenako, mwadzidzidzi, apa unabwera Mzimu Woyera uwu kuchokera Kumwamba, ndipo Iwo unawafulumizitsa iwo. Ndipo kufulumizitsa kunachitika, iwo sanachite mantha kuti akachitire umboni Uthenga umene iwo ankawukhulupirira ndipo ankawudziwa kuti ndi Choonadi. Apo ayi, iwo ankawuwopa Iwo.

141 Ndi Apresbateria angati, Amethodisti angati, Abaptisti angati, mdziko lero, ndi Achipentekoste angati, amene amadziwa Choonadi ndipo amachita mantha kuti ayime pa Icho? Ine ndikukakamizidwa kudabwa, ndi chiyani chimene chinakugwerani inu? Kodi ndinu gawo la chiwukitsiro Chake? Kodi mungayerekeze kufuula chifukwa cha chiphunzitso ndi lingaliro la munthu wina? Kapena, muli nako kulimba mtima kwenikweni ndi—umuna weniweni umene umatengera, kuti mungaimo ndi kuchitcha cholondola “cholondola,” ndi cholakwika “cholakwika”? Kodi ndinu gawo la chiwukitsiro Chake, kapena kodi ndinu wopembedza wa mulu wa tizikhulupiriro? Kodi ndinu wopita ku tchalitchi, kodi muli nalo dzina lanu pamene, ndipo mwafa mu tchimo ndi nzolakwa?

Iye amene sakhulupirira Mawu athunthu a Mulungu ndi wochimwa.

142 Afarisi amenewo ankakhulupirira zinthu zambiri, kuti ndi Choonadi. Iwo anati, “Ndife ana a Mulungu.” Ndipo iwo anali, mpaka Mawu amenewo analalikiidwa. Koma pamene Mawu amenewo analalikiidwa ndi kutsimikiziridwa, ndiye iwo anadzakhala ochimwa, chifukwa chokana Chinthu chimene iwo ankachidziwa kuti chinali cholondola, ndipo anachitira umboni zimenezo. “Ife tikudziwa kuti Inu ndi mphunzitsi wochokera kwa Mulungu, pakuti palibe munthu angathe kuchita zinthu zimene Inu mukuchita popanda Mulungu kukhala ndi Inu.”

143 Ine ndikudabwa lero, kodi ife tiri pati? Ine ndikukufunsani inu. Kodi chiwukitsiro ichi chikutipeza kuti ife? Kodi mungayerekeze kutuluka panja? Kodi mungayerekeze kumutenga Mulungu pa Mawu Ake? Ngati ndinu wodzozedwera ku Moyo, inu ndithudi mudzachita zimenezo. Ngati ndinu mphungu, inu simungadziletse kuchita zimenezo, muli Chinachake mwa inu. Kapena, kodi mukungofuna kutumikira kachikhulupiriro kwina, kumati, “Ndimapita ku tchalitchi. Ndine wabwino basi monga inu muli”? Mukuona? Ngati mulibe ufulu wakubadwa, inu simudzawuwona konse iwo, inu simungawuwone iwo. Koma ngati mukugwirizira ufulu wakubadwa uwu, simungadziletse kuwona izo, chifukwa ndi gawo la inu ndipo ndinu gawo la izo.

144 Ine ndingawakane bwanji amayi amene anandibala ine? Ine ndingawakane bwanji abambo, amene magazi awo omwe ali mwa ine? Ine ndingamukane bwanji Charles Branham kukhala abambo anga? Ine sindingachite zimenezo. Ndine wololera kupirira chitonzo chake kapena china chirichonse, chifukwa ndine mwana wake. Aleluya!

145 Ndiye pokhala mwana wa Mulungu, ndipo Iye anali Mawu a Mulungu, ine ndingalikane bwanji Baibulo limenelo kuti ndi Choonadi, kuti Yesu Khristu sali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Ndi kuwona ora limene ife tikukhalamo, ife tikusowa Isitara mu mpingo. Chiukitsiro! Ife tikusowa chiwukitsiro, kuti chilimbitse chikhulupiro, amuna ndi akazi kuti aziyimirira icho chimene chiri Mawu otsimikiziridwa a Mulungu.

146 Mukuti, “Chabwino, ife tikuwapangitsa Achinyamata athu kukhala a Khristu.” Zonsezo nzabwino. “Mpingo wathu uli ndi msonkhano. Ife tikufuna mamembala ochuluka *chotere*.” Palibe chotsutsa izo. Izo zonse nzabwino. Koma ndi chikhalidwe chabe. Izo zikhoza kukhala nthenga zakale za nkuku. Koma ngati iwe ungafike mu chikhalidwe choyenera kumeneko, ilo lidzaswa mphungu ngati liri dzira la mphungu. Ndipo ngati inu munakozedweratu ndi Mulungu kuti mudzawone izo, inu simungathe kudziletsa kuwona izo, inu mudzatulukira mu chiukitsiro. Umo ndi momwe Abaptisti anabadwira, umu ndi momwe Amethodisti anabadwira, mu chiukitsiro cha tsiku limenelo, koma iwo anatembenukira kwa nkuku mmalo mwa mphungu.

147 Monga ine ndinanena osati kale kwambiri, popita uko ndikuchokera ku Tucson, ine ndinawona chinthu chachirendo kwambiri. Ine ndinawona khwangwala atakhala pa waya kumusi uko. Khwangwala ameneyo anataya kale chomuzindikiritsa chake. Iye kalelo anali mbalame ya pafupi ndi mphungu. Iye sangakwanitse kutsatira mphungu; ayi, mwa njira iliyonse. Palibe chimene chingatsatire mphungu. Koma iye anali khwangwala.

148 Khristu ndi Mphungu, ndipo mpingo ukuyenera kukhala mwina khwangwala. Iwo amatha kuuluka mmwamba kuposa mbalame zina zonse. Koma khwangwala ameneyo wasanduka wofewa. Iye wataya chomuzindikiritsa chake. Iye akumakhala pa mawaya a telefoni ndi kumadikirira kalulu wina wakufa. Iye akumalumpha ngati mwimba, mmalo mowuluka ngati khwangwala.

149 Oh, m'bale wanga, mlongo, inu anthu Achipentekoste, amene muli anthu anga omwe okondedwa! Mpingo ukutaya chowuzindikiritsa chake. Iwo ukubwera chotsika ndipo ukudalira kachikhulupiro kena kakufa, mmalo mowulukira mu Zakumwamba, kutali, kukapeza manna atsopano.

¹⁵⁰ Khwangwala anakonda kumakasaka manna ake omwe, koma lero iye akumatenga zimene galimoto zaponda ndi zimene mwimba ikumadya. Iye amalumphu ngati iyo. Iye amawoneka ngati iyo.

¹⁵¹ Ife timadzikongoletsa tokha kwambiri mu dziko lamakono, akazi athu akumameta tsitsi lawo, ndi kumavala akabudula, amuna athu alibe nsana wokwanira kuti ayime pa guwa ndi kunena zoon. Ife tinakhala kale ofewa pa Mawu.

¹⁵² O Mulungu, tumizani Mzimu Woyera ndipo mukafunefune mphungu zimenezo kwinakwake, zimene zakonzeka kukayima kutsidyako, ziribe kanthu chimene chingachitike, zimene zingawuluke kupita kosadziwikako, osati kukhala pa mawaya a telefoni ndi kumafunafuna mabuku ena a Sande sukulu kuti abweremo. Ndiloleni ine ndikhale nawo Mawu, ndipo mu utsopano wa mphamvu ndi chiwonetsero cha Mzimu Woyera. Ife tikusowa Isitara, chiwukitsiro chimene chiri chogwirizitsa. Mzanga, ngati iwe ukukhutsidwa ndi zovunda zoterezo za mdziko, pali chinachake cholakwika.

¹⁵³ Mlongo wanga, m'bale wanga, mundilole ndinene kwa inu, ichi, mmantha aumulungu, podziwa kuti ndikhoza osadzakhala ndi moyo kuti ndidzawone Isitara kachiwiri. Koma pali chinthu chimodzi chotsimikizika, pamene mwana weniweni wodzozedweratu wa Mulungu, mwa Mawu a Mulungu, amva Liwu limenelo la Mulungu, iye adzawuka ndi kupita kukakomana ndi Ilo. Ndi zogwirizitsa, kuti akukakomana ndi Mawu enieni amoyo. Monga Iye anali, Mkwatibwi adzakomana ndi Mkwati. Iye ndi gawo la Thupi Lake.

¹⁵⁴ Zindikirani, takhalapo motalika, tikutaya zotizindikiritsa zathu. Ife timabwera Lachitatu usiku, ena a ife. Ena amakhala kunyumba kuti awonere *Ndani Amamukonda Susie*, matelevizioni, mitundu yonse ya zinthu za mdziko, mitundu yonse ya zosangalatsa, kuti zikupititseni kutali ndi tchalitchi. Tinataya izo kalekale.

¹⁵⁵ Maseminare athu, masukulu athu, akutulutsa gulu la ma Ricky ndi zafioloje zochuluka, ndi—ndi zosangalatsa ndi chirichonse mu mpingo, kuti zikatenge malo a msonkhano wa pemphero. Taitenga diresi ndipo tayeretsa kukwaniritsa chimene amakono akuyesetsa kuchita, kuwabweretsa iwo mmenemo. Inu simudzawapindula konse iwo ndi zimenezo. Iwo ali nazo zochuluka za izo kuposa zimene inu muli nazo. Mulibe chochita pamalo anu. . . pa malo awo. Aloleni iwo abwere kwa anuwo, kumene ubatizo weniweni ukuwala, kumene mphamvu yeniyeni ya chiwukitsiro. Musayesere kumanga tchalitchi chofanana ndi chawocho. Musayesere kukhala ndi m'busa monga ameneyo. Musayesere kuchita *ichi*, *icho*, *china*, kapena kugwirizana ndi dziko. Iwo amanyezimira ndi Hollywood.

¹⁵⁶ Uthenga weniweni umawala ndi mphamvu. Mphungu zimamva zimenezo. Izo sizimafunafuna kunyezimira. Izo zimafunafuna kuwala. Kuwala ndi kudzichepetsa, kuwala ndi chikondi, kuwala ndi mphamvu, icho ndi chimene mphungu yeniyeni imasaka. Inu simungakapalase mu khola ndi kumukondweretsa iye. Iye sadzakwanitsa konse kuchita zimenezo. Inu simunganene izo kwa iye, chifukwa iye samakhulupirira izo.

¹⁵⁷ Mulole Liwu limenelo lifuule kuchokera Kumwamba, “Ine ndi Iye amene ndinali wakufa, ndipo ndiri wamoyo kenanso.” Chinachake chikuchitika. “Ine ndine yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo zidzachitika mmasiku otsiriza, Ine ndidzadzitsanulira cha Inemwini pa mnofu wonse.” Ulemelero kwa Mulungu! “Ndidzafulumizitsa chinenero chanu chachivundi. Ine ndidzafulumizitsa malirime anu achivundi. Ine ndidzakupatsani inu umboni wakuti Ine ndidzakubweretsani inu mu chiwukitsiro limodzi ndi Ine.” Mphungu za mtima wanjala zimafikira zimenezo mwamphamvu basi momwe zingathere. Ndi Ngale ya mtengo wapatali, kuti amagulitsa china chirichonse, kuti apite kukagula. Amenii.

¹⁵⁸ Mulungu atithandize ife, mzanga. Mipingo yathu ikutaya chowazindikiritsa chawo.

Tiyeni tsopano tipite kwa ena.

¹⁵⁹ Taonani machitidwe a ophunzira amenewo, amantha. Iwo ankadziwa kuti Yesu anali Choonadi, koma, inu mwaona, Izo zinali zotsutsana ndi lingaliro lotchuka, chipembedzo chotchuka cha oralo, chipembedzo chosamalitsa kwambiri, Sar- . . . Afarisi, Asaduki, ndi ena otero, miyambo yawo, mafuko, ndi zipembedzo. Iwo anali—iwo ankatsutsana nawo “mpatukowo.” Koma Yesu anali Mawu ozindikiritsidwa.

¹⁶⁰ Ndipo Yesu ndi Mzimu Woyera, mu Mzimu. “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine. Inu mudzandiwona Ine,” osati thupilo; Moyo umene unali mwa Iye. Mulungu ali pa Mpingo, kuti akayitane ana aamuna monga Iye ankachitira kumeneko, omvera.

¹⁶¹ “Ine nthawizonse ndimachita chimene chiri chokondweretsa kwa Atate Anga. Ndani wa inu amene anganditsutse Ine za tchimo?” Mwakuyankhula kwina, *tchimo* ndi “kusakhulupirira.” “Kodi Mawu anena chiyani za Ine, zomwe sindinachite?” Ndi zimenezotu. “Ndiwonetseni Ine chimene Mawu ananena kuti Ine ndikanadzachita, chimene Ine sindinachite. Ndani anganditsutse Ine? Ndani angayike zala zanu pa Ine, ndi kunena kuti Ine sindinakwaniritse Mawu a Atate Anga?” Oh, pamene mpingo wa Chipentekoste ufika pa malo amenewo! “Ndani anganditsutse Ine za kusakhulupirira?”

¹⁶² Oh, Akhristu, muzindikiritsidwe osati ngati khwangwala, koma mphungu. Khwangwala ameneyo ndi wofewa, iye

adzatsika pansi. Inu simudzawona konse mphungu ikuchita zimenezo. Iyo siyidzachita konse zimenezo. Iyo imasaka chakudya chake chomwe, mosayembekezereka. Mulungu anayikonzekeretsa iyo kuti iziwona izo. Iyo imapeza mana atsopano, osati chinachake chimene chafa.

¹⁶³ Mu Ahebri, pamene iwo anawoloka kudutsa mchipululu, iwo ankadya, anayesera kudya manna akufa. Iwo anali atavunda. Iwo anali—iwo anali ndi mbululu mkati mwake. Inu mukudziwa chimene ife tikutanthauza. Iwo anangovunda basi, atawola. Mphutsi ziri mmenemo.

¹⁶⁴ Ine ndingadyerenji chakudya chimene chinafa zaka zapitazo? Chikhoza kukhala kuti chikuwoneka bwino, koma icho si chatsopano. Ife tikuyenera kupeza chakudya kam’badwo kalikonse, chatsopano. Chomwechonso mphungu imafunafuna chakudya chimenecho, kam’badwo kalikonse, monga ife tiri mu ulendo wathu. Zindikirani.

¹⁶⁵ Tsopano tiyeni titenge anthu ena kenanso. Tiyeni titenge ena mwa aneneri a Chipangano Chakale, tiwone chimene iwo anachita.

¹⁶⁶ Tiyeni timuwone poyamba Stefano, momwe Stefano pakati pa Khonsolo ya Sanihedirini ija. Pamene bungwe lija linamubweretsa iye kumeneko, gulu lalikulu lija la okhulupirira kumeneko, kapena ankayenera kukhala okhulupirira, anamubweretsa iye ndipo anayesetsa kumutsutsa iye. “Bwanji,” iye anati, “inu owuma makosi, osadulidwa mu mtima ndi mmakutu, inu nthawizonse mumaukaniza Mzimu Woyera.” Ndiwo Moyo Wamuyaya uja. “Monga makolo anu anachitira mmbuyomo kupyolera mwa aneneri, chomwechonso inu mukuchita izo lero.” Ndipo anakukuta pa iye ndi mano awo. Sanafune kumva zimenezo. Iye ankatsutsana ndi kachikhulupiriro kawo. Iye ankatsutsa chipembedzo chawo. Ndipo anamugenda munthuyo mpaka anafa. Ndipo anakwezera manja ake mmwamba, anayang’ana Kumwamba, anati, “Ndikuwona miyamba yatseguka, ndipo Yesu akuima padzanja lamanja.” Bwanji? Iye anali ndi chiwukitsiro, mphamvu yofulumizitsa mwa iye, imene inamutengera iye mu zifuwa za Yesu.

¹⁶⁷ Zindikirani, mwamsanga tsopano. Tayang’anani pa Filipino, kumusi uko mu chitsitsimutso chachikulu. Akukhala ndi chitsitsimutso kumene kunali kosatheka kwa munthu aliyense, bwanji, ngati iye akanakhala ndi mgwirizano waukulu pakati pa matchalitchi ndi chirichonse kumusi kumeneko. Anali ndi chitsitsimutso chachikulu. Ndipo mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu inayankhula kwa iye, inati, “Stefano. . .” Mwina Iyo inanena ichi, “Iwe ukukhala ndi chitsitsimutso chachikulu, koma ine ndiri ndi mwamuna mmodzi amene ndikufuna kuti iwe uyankhule naye.”

168 Ndipo Stefano ndi womvera, ziribe kanthu chimene icho chiri, kutsutsidwa kochuluka bwanji. “Oh, a Stefano, sungathe kuchokapo.”

“Koma, ine ndikhoza. Mulungu ananena chomwecho.”

169 Ndipo anatuluka kupita mchipululu, ndipo kunjako anamupeza mdindo uyu. Ndipo chinachitika ndi chiyani? Iye anati, “Wachita... Ngati iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse, kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu, ine ndikubatiza iwe.” Pamene iye anamubatiza iye...

170 Penyani. Iye anafulumizitsidwa ndi mphamvu yofulumizitsa iyi, kusiya chitsitsimutso cha anthu masauzande, kupita mchipululu, kwa munthu mmodzi. Oh, izo zikanakhala zotsutsana ndi zifukwa zonse. Mukuona? “Bwanji, pali teni sauzande akukufunani inu *kuno*.” Koma kuli mmodzi amene akufuna, kunja *uko*. Mukuona? Ndipo mphamvu yofulumizitsa inamutumiza iye ku malo operekedwa ndi Mulungu. Aleluya!

171 Amuna ndi akazi, Iyo idzakupangitsani inu kuyima pa mapazi anu. Iyo idzakupangitsani inu kuchita zinthu zimene Mulungu akufuna kuti inu muchite. Ine sindikusamala chimene wina akunena za izo. Woyandikana naye akuti, “Oh, munthu ameneyo wasokonezeka maganizo. Akupemphera usiku wonse; iwo amawerenga Baibulo.” Ine sindikusamala zimene iwo akunena. Ndi chimene Mulungu anakuitanirani inu kuti mudzachite. Ndiko kulondola. “Oh, iwo amati ife sitingakhale ndi zitsitsimutso zachikale izi, za Chipentekoste.” Oh, inde, ife tikhoza, nafenso. Inu mukhoza kukhala nazo izo mwa inunokha. Ndipo inu ndi ochuluka, mwa Mulungu, ziribe kanthu chimene ena a iwo akuganiza.

172 Zindikirani, zitatha, mu kumvera. Mvetserani mwatcheru tsopano. Atatha kumumvera Mulungu, ku Mawu Ake, pamene iye anakwaniritsa ntchito yake, mphamvu yofulumizitsa iyo imene iye anailandira pa Pentekoste inamutengera iye kutali, inafulumizitsa thupi lake. Mailosi ndi mailosi kutali, iye anatungedwera mu Mzimu, ndipo anakapezeka ali ku dziko lina kwinakwake. Mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu! Ndipo ngati ife tiri achipentekoste, “Mphamvu yomweyo imene inamuwukitsa Yesu kwa akufa, ngati Iyo ikukhala mmatupi anu achivundi.” Mukuona? Chabwino. Zindikirani.

173 Tiyeni timutenge munthu wina amene anakhala ndi mphamvu yofulumizitsa iyi. Panali munthu kalekale, dzina lake Enoki. Pamene chinthu chatsopano chinabwera, pamene chinachake chinabwerapo ndipo chinati, “Chabwino, tsopano ife tikuyenera kubwerera ku sukulu yakale, kapena *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*,” Enoki anayenda ndi Mulungu. Chirichonse chimene Mulungu anati achite, Enoki sanaphonye Mawu amodzi. Iye ankayenda ndi Mulungu. Kodi iye anali chiyani?

Iye anali mwana wa Mulungu. Iye anali mphungu imene inaitanidwira tsiku limenelo.

¹⁷⁴ Ndipo pamene nthawi inadzafika, iye anali wodzaza kwambiri ndi mphamvu yofulumizitsa imeneyo! Kumbukirani, iye anali atayenda zaka faivi handirede, kapena zochulukirapo, pamaso pa Mulungu, ndipo panalibe nthawi imodzi imene iye anaphonya Mawu Ake. Palibe nthawi imodzi imene iye sanakhale khalidwe labwino. Palibe nthawi imodzi imene iye anachita koma kusunga umboni. Chirichonse chimene Mulungu anamuuza iye kuti achite, iye anapita ndi kukachichita icho. Panalibe kukangana nazo izo, iye anangopita kukachita izo. Ziribe kanthu chimene wina aliylene ankaganiza, iye anapita ndi kukachita izo. Chifukwa chiyani? Iye anali wodzaza ndi mphamvu yofulumizitsa imeneyo. Ndipo pamene inafika nthawi yoti munthu wokalambayo afe, Mulungu anangotsitsa makwerero ndipo iye anakwera kupita Kwawo. Iye anamufulumizitsa iye, ndipo anatengera thupi lake lachivundi mmwamba mu mkwatulo. Amen. Imeneyo ndi mphamvu yofulumizitsa ija.

¹⁷⁵ Tayang'anani pa Eliya, ntchito yake itatha pa dziko lapansi. Iye anali wokhuta kwambiri ndi mphamvu yofulumizitsa imeneyo, iye anawatsutsa mamededwe a Jackie Kennedy amenewo mu tsiku lake. Iye anali atamuuza Yezebeli wokalamba zimene iye ankaganiza za iye. Iye anawauza alaliki amenewo ndi anembe chimene chinali chabwino ndi choyipa, ndipo iwo sanamukhulupirire iye. Koma iye anawadzudzula akazi openta nkhope amenewo ndi zinthu, moyipa kwambiri. Ndipo iye atakhuta kwambiri mphamvu yofulumizitsa imeneyo mpaka panalibe chimene chikanamuvulaza iye. Mulungu anali atamudyetsa iye kuchokera mmiyamba, anamutulutsako iye ndipo anakamuika iye pambali. Ndipo iye anali atakhuta kwambiri mphamvu yofulumizitsa, inafika nthawi yoti afe, Yordani anatseguka, ndipo iye anangoyenda, anatsitsa galeta ndipo anamutengera iye Kwawo, atakhuta kwambiri mphamvu yofulumizitsa imeneyo. Iye anakhala woona, mwana weniweni wa Mulungu. Eya.

¹⁷⁶ Zindikirani, iye anali ndi wolowa mmalo, ndipo dzina lake anali Elisha. Ndipo Elisha anali ndi magawo awiri, mphamvu yofulumizitsa iyi. Mukuona? Iye anali ndi magawo awiri a iyo. Tsopano, iye analalikira kwa pafupifupi zaka eyite, kapena iye anali pafupifupi usinkhu wa zaka eyite. Iye anadwala ndipo anafa. Tsopano, iye sanapite Kwawo monga Eliya anachitira. Mukuona? Awiri onsewo akuyimiridwa mmenemo mu Mpingo; oyera ena amapita, ndipo ena akupumula. Koma zindikirani pamene Eliya anatengedwera mmwamba mu mkwatulo; ndiye Elisha anakagona, mwa Mulungu, atakhuta mphamvu yofulumizitsa. Tayang'anani pa uneneri wake iye asanafe. Mukuona?

¹⁷⁷ Tsopano, ndiloleni ine ndikuwonetseni inu. Ine sindikusamala ngati inu muli wakufa, kapena kumene inu muli, mphamvu yofulumizitsa imeneyo sichokapo. Zaka ndi zaka pambuyo pa imfa yake, nyama yake inali itavunda, mphutsi zapakhungu zinali zitayidya iyo. Koma iwo anali atanyamula munthu wakufa, tsiku lina, anamuponyera iye pa mafupa amenewo, ndipo pamenepo panali mphamvu yofulumizitsa yochuluka mpaka munthuyo anabwerera ku moyo kenanso. Aleluya! Anamuukitsa iye kwa akufa, chifukwa mphamvu yofulumizitsa ija imene inali pa woyera wa Mulungu ameneyo, sinamusiye konse iye, inatsalira mmafupa amenewo.

¹⁷⁸ Oh, kumbukirani, ife ndi mnofu wa mnofu Wake, fupa la mafupa Ake, ngati ife tiri Mkwatibwi Wake. Imfa sidzavutitsa mphamvu yofulumizitsa imeneyo nkomwe. “Ngakhale mphutsi za mthupi zitawononga thupi ili, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu.” Ulemelero kwa Mulungu! Chimene a...Sindikudziwa chimene ndinganene. Ndi chiyembekezo bwanji kwa bambo wachikulire monga ine, podziwa kuti ndikuwona kutha kwa nthawi yanga kutaliko posachedwapa, ngati usinkhu wa zaka fifite-sikisi.

¹⁷⁹ Kuyambira ndiri mnyamata wamng’ono kwambiri ine ndayima pano, kuyesetsa kuti ndilengeze Ichi. Koma ndikudziwa kuti mwa ine, mulibe chabwino chimene ndiri nacho, palibe chimene ndachita, koma mwa ine muli mphamvu yofulumizitsa ija; iyo inandifulumizitsa ine tsiku lina kuchoka ku zinthu za mdziko, ngati mnyamata, kupita ku Moyo Wamuyaya. Oh, zinthu zimene zachitika! Ine ndawonapo masomphenya, ndanenerapotu zinthu. Iye sanalole kalikonse kuti kalephere. Ine ndayankhulapo mmalirime ena. Ine ndanenerapo. Ine ndachitapo zinthu zimenezo mwa Mzimu wa Mulungu umene umakhala mwa ine. Ndiyo mphamvu yofulumizitsa. Ndikudziwa kuti tsiku lina . . .

¹⁸⁰ Muwomboli wanga ali moyo tsopano. Ndipo tsiku lina pamene Iye adzabwera, mafupa awa adzawuka kenanso, kuti apite kukakomana naye Iye mu mlengalenga. Inu mukhoza kundiika ine mnyanja, kulitentha ilo, kulikonse kumene inu mukufuna. Mphamvu yofulumizitsa imeneyo ndi Yamuyaya. Psyii! Ine ndikumverera Isitara pakali pano. Inde, bwana. Ndakhala nayo kwa zaka. Ili mwa ine.

¹⁸¹ Ili mwa inu. Ngati, inu, Mzimu umene unamuwukitsa Yesu kwa akufa ukhala mmatupi anu akufa, Iwo wakufulumizitsani inu ku zinthu za mdziko, kupita ku Mawu a Mulungu okha. Iwo wakufulumizitsani inu kuchoka ku moyo uno kupita ku Moyo Wamuyaya. Inu amene munali akufa mu tchimo ndi nzolakwa tsopano mwafulumizitsidwa pamodzi, kuti mukakhale mmalo a Mmwambamwamba pamodzi ndi Khristu Yesu, kuseyama pa Manna ochokera Kumwamba, kuwona dzanja la Mulungu likuwonetseredwa, kutsimikizira lonjezo la tsiku lino.

182 “Monga zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu. Iwo ankadya, kumwa, kukwatira, kuperekedwa mu kukwatiwa. Ndipo monga zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala mu maora amene Mwana wa munthu adzaululidwa padziko lapansi,” osati Mwana wa Mulungu, kenanso. “Mwana wa munthu,” kubwerera ngati Uthenga wauneneri wa tsiku lotsiriza pamene mphungu imeneyo idzakhala ikuwuluka; osati mkango; osati ng’ombe mu m’badwo wa nsembe. Mukuona?

183 Nthawi iliyonse, ulamuliro wachipembedzo unkapita kukakumana ndi chitsutso cha ulamuliro wandale cha mdziko. Pamene mkango unadzuka, mphamvu yachipembedzo, iyo inapita kukakomana ndi mphamvu ya Chiroma.

184 Ndipo kenako pamene linafika ora lansembe, ng’ombe inapita, chifukwa iyo ndi Chamoyo chansembe cha Ambuye.

185 Kenako panabwera okonzanso, kutsika kudutsa mu mibadwo ya mpingo, kunabwera nkhope ya munthu. Ndipo okonzanso analipo kuyambira kwa Luther, Wesley, oh, Calvin, kupitirira mpaka mmusi, mmusi, m’badwo wa chipentekoste.

186 Koma mu Uthenga wotsiriza umene unapita, kunabwera mphungu yowuluka. Ndi nthawi ya mphungu, nthawi yowulula, Mawu a Mulungu akuwonetseredwa, Mawu a Mulungu kutsimikiziridwa. Oh, ana, yendani kulowa mu ubatizo wa Mzimu Woyera uwu. Dzaloweni ndipo mudzakhulupirire Izo, ndi mtima wanu wonse, Mulungu akudzazani inu.

187 Taonani apa tsopano. Tikupeza tsopano, kumbukirani, “Ndife mnofu wa mnofu Wake, ndi fupa la fupa Lake.” Monga Mulungu anawukitsa mafupa ndi mnofu Wake kuchokera mmanda, iwo sangathe kumubisa munthu amene ali ndi zogwirizitsa. Imfa siingathe kumutenga iye. Yesu anati, “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine. Ine ndidzawaukitsa iwo pa tsiku lotsiriza.” Oh, mai! Isitara! Bwanji, ife tiri mu Isitara kumene. Pamene Iye anawuka, ife tinauka ndi Iye. Iye anatumiza mtheradi. Ife tawugwirizira iwo, ngati ubatizo wa Mzimu Woyera. “Iye ndi wamoyo kosatha; yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ahebrei 13:8 amatsimikizira zimenezo. Iye ndi yemweyo.

188 Umesiya Wake, iwo odzozedwa amakhulupirira zimenezo. Kodi Mesiya ndi chiyani? Kodi Mesiya ndi chiyani? *Mesiya* ndi “Mmodzi wodzozedwayo.” Ndipo tsopano ngati Iye anali Mesiya, pokhala Mmodzi wodzozedwayo wa tsiku limenelo, kuti akakwaniritse Mawu a Mulungu, kuti adzakhale Muomboli ndi Wodzozedwayo, ndipo Mulungu anawukitsa thupi limenelo; Mkwatibwi Wake ndi wodzozedwa wa tsiku lino. Iwo anaukitsidwa kale ndi Iye mu chiukitsiro, chifukwa, “Awiriwa ndi mmodzi.” Amen.

189 Ine—ine ndikanakonda ndikananenera izo momwe ndikuziwonera izo. Ndikanakonda ndikanakhala ndi maphunziro amene ndikanachita ndi izo. Mukuona? Ine—ine ndikuyembekeza kuti inu mukuziwona izo. Ine ndikuyembekeza, Mulungu, Mzimu Woyera umatsika pamenepo ndipo umadzayika izo mu mtima mwanu, kuti muone chimene ine ndikutanthauza.

190 Chiukitsiro, ife tiri mu chiukitsiro tsopano. Ife tikukhala ndi Iye mu chiwukitsiro, koma iwo okha amene ali ndi Moyo.

191 Osati iwo amene alibe Moyo. Iwo sangawudziwe Iwo. Iwo sadzawudziwa konse Iwo. Iwo azidzapitirira kumaganiza kuti akulandira Mzimu Woyera, akupulumutsidwa, ndipo Mkwatulo udzakhala utatha ndipo wapita. Anati, “Eliya anabwera kale, ndipo iwo anachita mwanjira imeneyo, ndipo inu simunazidziwe izo.” Mukuona?

192 Zindikirani. Imfa simaimitsa mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu. Zindikirani. Imfa siingathe kuimitsa iyo.

193 Inu mukuti, “Chabwino, amayi anga anali mkazi wodzazidwa ndi Mzimu. Abambo anga, ine sindinamuwonapo mwamuna wodzaza ndi mphamvu monga abambo anga. Koma iwo anafa, M’bale Branham.” Ndithudi. Izo sizinaititse mphamvu yofulumizitsa.

194 Mose anali nayo mphamvu yofulumizitsa imeneyo. Inu mukukhulupirira zimenezo? Panali pasanakhalepo munthu wonga iye pa dziko lapansi, mpaka Yesu. Pakuti iye sanangowona masomphenya kokha, an kayankhulana maso ndi maso ndi Mulungu.

195 Ngakhale mneneri wamkazi, Miriamu, anatsutsa mawu ake tsiku lina. Iye anati, “Kodi iwe sumamuwopa Mulungu? Umulingalire mtumiki wanga, Mose. Palibe wina mdziko wonga iye, ora lino. Sipanayambe pakhalapo aliyense wonga Mose. Ine ndimayankhula ndi Mose. Kodi iye ananena chiyani, chimene sichinali choonadi? Mukuona? Ine ndimayankhula ndi Mose. Kodi iwe sukumuwopa Mulungu? Usanene mawu omutsutsa iye.” Ndipo pomwepo iye anakanthidwa ndi khate—ndipo amafa. Iye sanakhale moyo nthawi yaitali, pambuyo pake. Mose anamupempherera iye.

196 Ndipo Mose anakwera pamwamba pa phiri, pa zaka handirede ndi twente za utumiki, kapena zaka eyite za utumiki; zaka handirede ndi twente za moyo, anakwera pamwamba pa mapiri ndipo anakafa, ndipo anakaikidwa mchigwa. Koma mphamvu yofulumizitsayo inali pa iye. Pafupifupi zaka eyiti handirede zitapita, ndi uyu apa, atayima pa Phiri la Chiwalitsiro. Amen. Kodi iye anali chiyani? Iye anaphatikizidwa mu chiwukitsiro chimenecho. Ndithudi, iye anali. Iye anali ndi mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu. Apa iye anali, atayima.

¹⁹⁷ Tamuwonani Yobu, Abrahamu, Isaki, oyera pa tsiku la chiwukitsiro, mmawa waukulu uja umene Yobu ndi onse a iwo ankadziwa kuti ukanadzabwera. Pamene, iye anati, “Ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo,” mahandirede ndi mahandirede a zaka Khristu asanabwere. Ilo, kwenikweni, Bukhu la Yobu linalembedwa Genesis asanakhalepo, iwo amatero, Bukhu lakale kwambiri mu Baibulo.

¹⁹⁸ Ndipo mu mayesero ake, ndipo monga ife tikudutsamo tsopano. Ndipo mkazi wake, ngakhale, chinthu chapafupi kwambiri kwa iye pa dziko lapansi, anati, “Bwanji osamutukwana Mulungu ndi kufa imfa?”

¹⁹⁹ Iye anati, “Iwe ukuyankhula ngati mkazi wopusa. Ambuye anapereka, Ambuye watenga, lidalitsike Dzina la Yehova.”

²⁰⁰ Ndipo kenako pamene Mzimu wa Mulungu unadza pa iye, ndipo iye anayamba kunenera, iye anati, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo, ndipo pa masiku otsiriza Iye adzayima pa dziko lapansi lino. Ngakhale mphutsi za mthupi zitawononga thupi ili, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu.” Ndipo iye anapanga malo oti adzadziyikepo yekha. Iye anati, “Tigula malo awa.” Anagula kumeneko ndipo anadziika yekha.

²⁰¹ Pambuyo pake, kunadzabwera mwamuna wotchedwa Abrahamu. Mpingo ukukula, ukubwera mmwamba. Abrahamu, chabwino, tsopano, iye anali ndi zogwirizitsa za Mulungu, nayenso, Moyo wosatha, Wamuyaya, chifukwa Mulungu anamuyitana iye. Tsopano zindikirani. Pamene iye anafa, kapena Sarah atafa, iye anagula kachidutswa ka malo mu Palestina, pafupi ndi manda a Yobu, ndipo anamuika Sarah. Abrahamu anamwalira ndipo anaikidwa mmanda pamodzi ndi Sarah. Abrahamu anabala—anabala Isaki.

²⁰² Ndipo Isaki, pamene iye anafa, iye anagona ndi Abrahamu, mu gawo lomwelo la nthaka. Tsopano, pamene, Isaki anabala Yakobo . . .

²⁰³ Yakobo anafera, kutali komwe mu Igupto. Koma pokhala mneneri, tsopano, ndi chogwirizitsa ichi, mphamvu yofulumizitsa iyi, iye anati, “Usadzandiike ine kuno, Yosefe. Bwera kuno, mwana wanga mneneri. Ika dzanja lako pa ntchafu iyi imene Mulungu anailumalitsa. Ulumbire kwa Mulungu wa Kumwamba kuti sudzandiika ine kuno.” Kodi munali chiyani mwa munthu ameneyo? Chifukwa chiyani Igupto sikunali kwabwino basi ngati malo aliwonse? Iye anali mneneri. Iye ankadziwa kumene chiwukitsiro chimenecho chikanati chidzachtikire. Sikuti kukanakakhala ku Igupto; kukanakakhala ku Palestina. Anati, “Ika manja ako pa ntchafu yanga yolumala, ndipo iwe ulumbire pa Mulungu amene ndamutumikira. Ndiwe mwana wanga mneneri, kuti,

sudzayika mafupa anga kumusi kuno. Udzanditengere ine uko ndi kukandiikako ine.”

²⁰⁴ Yosefe, pokhala mneneri, nayenso, anaika manja ake pa abambo ake olumala. Anati, “Ndikulumbira pa Mulungu wa Abrahamu, Isaki, wa Yakobo, sindidzakuikani inu kuno.” Iwo anamutenga iye ndipo anakamuika iye mu dziko limenelo. Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani?

²⁰⁵ Pamene Yosefe anamwalira, iye anati, “Musadzandiike ine kumusi kuno. Musadzandiike ine kumusi kuno.” Chifukwa chiyani? Mulungu ndi Mulungu paliponse, koma Iye amakhala ndi dongosolo. Yosefe anali mneneri. Iye anati, “Tsiku lina,” mvetserani, mawu ake, “Ambuye Mulungu adzabwe-... adzakuhezzerani inu, ndipo adzakutulutsani inu mu dziko lino. Ndipo pamene muzidzapita, mudzatenge mafupa anga.”

²⁰⁶ Mphamvu yofulumizitsa ija inali mmafupa amenewo. Oh! “Ngati Mzimu wa Iye amene anawukitsa Khristu kwa akufa, ukhala mwa inu, Iye aponso adzafulumizitsa matupi anu achivundi.”

²⁰⁷ “Musadzaike mafupa anga kumusi kuno. Mudzawaike iwo kumtunda uko ndi awo a lonjezo.”

²⁰⁸ Pamene Yesu anabwera, apa, ine ndiri ndi Lemba apa, Mateyu 27:51. Pamene Yesu anauka kwa akufa, Yobu anaziwona izo zikubwera, anati, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo. Masiku otsiriza, Iye adzaima pa dziko lapansi ili. Ngakhale mphutsi zapa khungu zitawononga thupi ili, komabe mthupi langa ine ndidzamuwona Mulungu. Ine ndidzamuwona Iye.” Iwo anakadziwa. Ameneyo anali mneneri. Abrahamu anali mneneri. Isaki anali mneneri. Yakobo anali mneneri. Yosefe anali mneneri. Ndipo iwo anali ndi vumbulutso la Mulungu, mogwirizana ndi Mawu Ake. Ndipo pa mmawa wa Isitara umenewo, pamene Mmodziyo anabwera ndi kudzawawombola onse amene anakhulupirira pa Iye, iwo anauka, nawonso, mogwirizana ndi Baibulo.

²⁰⁹ Mphamvu yofulumizitsa imeneyo inabwera mmanda a Yobu, kumene kunalibe ngakhale fumbi lodzala mu supuni la mafupa ake litatsalira. Atadutsa mahandirede onse amenewo, ndi mahandirede, ndi mahandirede a zaka, mafupa ake anali atawola. Iwo—iwo anabwereranso mmbuyo, ndipo anabwereranso ku mipweya ya padziko lapansi, ndipo fumbi chabe la phulusa linali pamenepo. Koma, komabe, pamene mphamvu yofulumizitsa ija, mogwirizana ndi Mawu a Mulungu, kwa lonjezo, mahandirede ndi mahandirede, inde, zaka masauzande zitadutsa, pamene mphamvu yofulumizitsayo inadzatulutsidwa kuchokera mmanda; Yobu, Abrahamu, Isaki, Yakobo, onse a iwo, anadzatuluka mmanda limodzi ndi Iye.

²¹⁰ Baibulo linanena chomwecho. Mateyu Woyera, mutu wa 27 ndi ndime ya 51, iyo inati, “Ambiri a oyera amene anagona mu

fumbi dziko lapansi, anawukitsidwa ndipo anatulukana mmanda limodzi ndi Iye, pamene Iye anabwera pa mmawa wa Isitara.” Chifukwa chiyani? Iwo anali ndi chogwirizitsa chimenecho. Iwo anali ndi mphamvu yofulumizitsa imeneyo, mwaona, ndipo anauka kwa akufa, ndipo anapita ndi Iye mu chiwukitsiro. Anasangalala ndi chiwukitsiro limodzi ndi Iye, chifukwa iwo anali atadzazidwa ndi mphamvu yofulumizitsa imeneyo. Iwo anali ndi chisindikizo chenicheni cha Isitara.

“Chabwino,” inu mukuti, “Ndikanakonda ndikanakhala mu Chipangano Chakale.”

²¹¹ Dikirani miniti. Mu Woyamba wa Atesal-...Atesalonika, mutu wa 4, ndime ya 16, ine ndikufuna inu kuti muwerenge zimenezo. “Ine sindikufuna kuti mukhale osadziwa, abale, za iwo amene akugona, kuti mungachite chisoni, ngakhale munga enawo amene alibe chiyembekezo. Pakuti ngati tikukulupirira kuti Yesu anafa, ndipo anaukansa tsiku lachitatu,” osati kudzipangitsa kukhulupirira, koma ife timakhulupirira zimenezo, “chomwechonso iwo amene akugona mwa Iye Mulungu adzawabweretsa pamodzi ndi Iye.”

²¹² Oyera a Chipangano Chatsopano ndi mphamvu yofulumizitsa imeneyo, adzauka, nawonso, pa Kudza Kwake kwachiwiri; motsimikiza munga oyera a Chipangano Chakale ndi mphamvu yonse yofulumizitsa pa mafupa awo, ndi kusandulika ndi mphamvu, ndi zina zotero, zimene zinawonetseredwa za Mulungu. Aneneri amenewo amene Mawu a Mulungu amadzako, iwo anawukitsidwa ndi Iye pa mmawa wa chiwukitsiro umenewo; ndipo ndi lonjezo la Mulungu kuti aliyense amene ali mwa Khristu Yesu adzabweranso ndi Iye mu chiwukitsiro Chake, mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu pa mafupa.

²¹³ Nzosadabwitsa, ife timaika manja pa odwala. Nzosadabwitsa, timakondana wina ndi mzake. Ndife abale ndi alongo. Ife tisamadane wina ndi mzake chifukwa timakonzedwa ndi Mawu a Mulungu. Ife tizikondana wina ndi mzake, ndi kumalemekezana wina ndi mzake. Inu mukudziwa, ngati simutero, izo sizidzakuthandizani inu.

²¹⁴ Pali munthu wamng’ono wakhala pomwe pano, amene, pansu pa mpingo uno tsopano. Masiku angapo apitawo... Munthu ameneyo amakhulupirira. Mnyamata wachikulire anali ndi khansa pa khutu lake, ndipo iye sakananana kanthu za izo. Iye ankagwira ntchito kumtunda uko ku nyumba. Ine ndinali pa ulendo wokasaka ndi iye, kumtunda uko ndi abale a Moseley, ndi M’bale Dawson kuno. Ife tinali kuno tikusaka, mwana wa M’bale William. Ndipo ine ndinapezeka ndikuyang’ana pa khutu lake, ndipo ine ndinaona khutu lake lonse litatupa. Ine ndinati, “Chavuta ndi chiyani, Donavon, khutu limenero?”

215 Iye anati, “M’bale Branham, izo zakhala ziripo kwa nthawi yaitali. Ine sindikudziwa.”

216 Ine basi—ndinangomugwira iye padzanja pamenepo. Imeneyo inali khansa yaikulu pa khutu lake. Sindinanenepo liwu limodzi; ndinangoligwira ilo, ndipo ndinaganiza, “M’bale wanga!” Tsiku limodzi kapena awiri zitachitika zimenezo, panalibe ngakhale chipsyera chotsalira pa ilo. Unali ulemu wake mwa Mulungu wa Kumwamba, ndi mphamvu Yake yofulumizitsa, zinapha khansa imeneyo ndipo zinapulumsa moyo wa Donavon Weerts kumbuyo uko. Uko nkulondola.

217 Kodi zinthu izi ndi ziti? Taonani kuno, anthu kuno mu Phoenix. Tayang’anani pa inu anthu amene mwakhulupirira izi. Tayang’anani pa anthu amene ali ndi ichi, amene amaika manja awo pa inu. Onani chimene chimachitika. Ndi mphamvu yofulumizitsa. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, mphamvu yofulumizitsa imeneyo, mphungu kwa mphungu, chinachake chichitika. Tsopano, mphungu kwa khwangwala, sizigwira ntchito. Mphungu kwa mphungu, imauka kuchokera ku khola, kupita ku Zakumwamba. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira,” pamene awiri onse ali mu zikhulupiriro.

218 Taonani mphamvu yofulumizitsa yomweyo ya Mulungu ikuimiridwa mwa aneneri awiri awa, Eliya ndi Elisha. Zindikirani, mawu omwewo; mmodzi wa iwo *akutengedwera mmwamba*, winayo *akukwatulidwira mmwamba*. *Kutengedwera mmwamba* ndi *kukwatulidwira mmwamba*. Mukuona? Iye anatengedwera mmwamba. Iye tidzatengedwera mmwamba; kutengedwera mmwamba ndi iwo, kukakumana nawo mu mlengalenga. “Kutengedwera mmwamba kukakumana nawo mu mlengalenga.”

219 Zindikirani, mbalame imayenera kukhala ndi mapiko awiri, kuti izizilinganiza yokha. Nkulondola uko? Eliya anali phiko lotanthauziridwa, Eliya. Elisha anali phiko la chiwukitsiro. Mukuona? Awiri onsewo, pamodzi, kuyimira oyera amene ali moyo ndi oyera amene anapita.

220 Kumbukirani, kufulumizitsidwa kuti awone zakale, makatani. Momwe anthu awa anafulumizitsidwira kumbuyo uko kuti awone kupyola katani ndi kudzawona pansu mu nthawi ino; aneneri amenewo!

221 Tayang’anani pa Paulo, ananena mu masiku otsiriza momwe anthu awa akanati adzakhaliye, kuchita ndi kudziticha okha Akhristu. Iye anali mneneri, wodzaza ndi mphamvu yofulumizitsa, anawoneratu izo zikukwaniritsidwa. Iye tikukhulupirira zimenezo. Sichoncho ife? Iye analandira mphamvu yofulumizitsa.

222 Tayang'anani pa mphamvu yofulumizitsa lero, ikuneneratu zinthu, popanda chochitika chimodzi chosowa. Popanda nthawi imodzi imene iyo imalephera. Mphamvu yofulumizitsa; osati mphamvu ya munthu; mphamvu ya Mulungu. Mphamvu, mtheradi wa Isitara, Yesu wowukitsidwayo amene anatumizanso mtheradi, kudzatitsimikizira ife kuti tinafulumizitsidwa kale ndi Iye.

223 Zindikirani. Inu mukukumbukira kabukhu kakang'ono, Amuna Amalonda pano, *Kuyang'ana Kupyola Katani La Nthawi?* Ine ndikuyamba kukalamba, podziwa kuti masiku anga akufupikira. Ine ndimapeza kwenikweni. . .

224 Ine ndimayimba kachidutswa kakang'ono kaja kamene madona awo anayimba kanthawi kapitako. Ndakhala nayo iyo kwa pafupifupi zaka eyitini, twente tsopano. *Ine Ndikufuna Tikambirane Izo, Ambuye.* Ndi kupita kunja uko ndi kuyamba kupemphera, ndikatero mphamvu yofulumizitsa ija imabwera. Ine ndapumula. Ine ndinayang'ana pamwamba Pamenepo. Ine ndinati, "Ndikuyang'ana kutali."

225 Ine ndikukumbukira mmawa umenewo, nditatengedwera kudutsa. Ndipo mkazi wanga, atakhala kumbuyo uko, atagona pa bedi yomweyo ndi ine mmawa umenewo. Ine ndinanyamulidwa mmwamba, ndipo ndinayang'ana mmwamba. Ndipo ndi uyo apo, akugona. Ine ndinati, "Ngati ine nditi ndichite chirichonse kwa Ambuye, iwe kulibwino ufulumire, mnyamata. Iwe wadutsa fifite." Kenako Mzimu Woyera unanditengera ine kutali, ndipo ndinayang'ana Kumeneko. Ine ndinawawona oyera amenewo, motsimikiza basi monga ine ndaima pano pa desiki iyi, ndi Bukhu lopatulika ili liri apa, ndi mtumiki wa Uthenga.

226 Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye koma chimene chinadzachitika? Ngati ine ndinatero, ine ndikufuna inu muniuze ine za icho. Nthawi iliyonse, kodi izo zakhala mwangwiro, pa nsanja? Nthawi iliyonse, kodi izo zinachitikapo monga momwe Iye ananenera? Ichi chinali PAKUTI ATERO AMBUYE.

227 Ine ndinayima pamenepo, ndinayang'ana pa nthawi imeneyo. Ine ndinawona ma teni amasauzande kuchulukitsa masauzande akubwera, amuna achichepere ndi akazi, akuthamanga, akuponya mikono yawo mondikumbatira ine, akukuwa. Ine ndinayang'ana kumbuyo ndipo ndinadziwona ndekha nditagona pabedi. "O Ambuye, ndiloleni ine ndiyang'ane kudutsa katani la nthawi."

228 Ndi chiyani chimenecho? Ndi mphamvu yofulumizitsa imene idzatitengere ife kutali. Mphamvu yofulumizitsa yayikulu imeneyo. Mphamvu yofulumizitsa inabwera mmasiku otsiriza ano.

229 Ndicho chimene ine ndadzera kuno ku Arizona, pakali pano. Pali anthu ambiri akhala pomwe pano, anayima pomwe pano ku Phoenix, ndipo anandimva ine ndikukuuzani inu kuchokera pa nsanja iyi, “PAKUTI ATERO AMBUYE.” Ndi angati akukumbukira zimenezo? “Tsopano pitani. Chinachake chikukonzekera kuti chichitike.”

230 Ine ndinawona Angelo seveni akubwera. Kodi *Life* magazini siinalemba zimenezo, pamene chifunga cha Iwo chinayandama modutsa apa, mailosi twente-seveni kutalika, ndi mailosi sarte chopingasa? Kodi si Fred Sothmann, ena awa, Gene Norman, iwo, akhala kumbuyo uko? Anayima pamenepo pamene Angelo seveni amenewo anawonekera pamenepo pa phiri. Izo zinagwedeza mapiri, kwa mailosi kuzungulira, monga choncho. Apo panayima Angelo seveni. Ndipo anaponya lupanga mdzanja lako, anati, “Pita kwanu ndipo ukatsegule Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiwi izi zimene zaperekedwa.” Ndipo ndi izi apa, chinsinsi choona cha chikwati ndi chilekano, ndi mbewu ya serpenti, ndi zinthu zonse izi zomwe akhala akukangana. Ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

231 Ndi chiyani chimenecho? Mphamvu yofulumizitsa ikubwera ku Mpingo, kumukonzekera Iye, ora lino limene ife tikuyandikira. Mphamvu yofulumizitsa!

O Mulungu, tithandizeni ife kuti tiilandire Iyo. Tithandizeni ife kuti tizikhulupirire Izo.

232 Mwaona, zimangotengera pa khalidwe limene inu mutengere kwa Izo, kaya Izo zikuchitirani inu ubwino uliwonse, kapena ayi, chonchobe. Mukuona? Inu mukuyenera kukhulupirira Zimenezo. Inu simukuzikhulupirira Izo, Izo sizingakuchitireni inu ubwino uliwonse.

233 Momwe Samuele wakale anaima pamenepo pamaso pa anthu amenewo, ndipo anati, “Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye koma chimene chinadzachitika? Kodi ine ndinayamba ndakupemphanipo inu ndalama zanu, kuti ndizikhulupirapo moyo?”

“Ayi, koma ife tikufuna mfumu, mulimonse.”

234 Umo ndi momwe mpingo uliri lero. Iwo akufuna malingaliro awo omwe. Iwo sangakhale ndi chidwi nkomwe pa iwe. Iwo amayenda mozungulira pamenepo. Chabwino, izo zimangowonetsera, mphamvu yofulumizitsa palibepo pamenepo.

235 “Oh,” inu mukuti, “Chabwino, ine ndinayankhula mmalirime. Ine ndinalumphu ndipo ndinafuula.” Ndizo zonse zabwino.

236 Koma ngati mphamvu yofulumizitsa iyo ili pamenepo, inu mudzazindikira. Monga mphungu yaing’ono ija; amenewo

ndi amayi ake. Amenewo ndi Mawu. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndi chimene Mulungu analonjeza. Ndi chimene chinanenedweratu. Ndicho ndendende chimene chinachitika. Ife tapyola mthunzi uliwonse wa kukaikira, mogwirizitsa tiri mu chiukitsiro pakali pano, oyera akukonzekera kunyamulidwa mmwamba.

²³⁷ Chotero, Yesu, wodzaza ndi mphamvu yofulumizitsa iyi, anati, “Ngati inu mungawononge kachisi uyu; amene anakutengerani inu zaka forte, inu munaganiza, kuti mumumange; Ine ndidzamudzutsanso iye mmasiku atatu.”

²³⁸ Chifukwa chiyani? Nchifukwa chiyani Yesu ananena zimenezo? Ndikufuna ndikufunsemi inu. Nchifukwa chiyani Yesu ananena chinthu choterocho? Iye ankadziwa Kuti Iye anali. Ameni. Ndikanakonda ndikanazipanga izo kukhazikika. Iye ankadziwa Yemwe Iye anali. Iye ankadziwa kuti, Mawu aliwonse, Mulungu anali atawalemba mmenemo za Iye, Iye anali atakwaniritsa izo. Iye ankadziwa kuti Iye anali Amene Davide ankamukamba.

²³⁹ Kodi inu mukudziwa kuti inu ndinu amene Baibulo limawakamba? Kodi inu mukudziwa kuti malo anu ali mwa Khristu? Ngati inu muli mwa Khristu, ndinu cholengedwa chatsopano. Kodi mukudziwa kuti Mawu awa ali ngati moyo wa tsiku ndi tsiku, kwa inu? Bwanji, ndithudi. Ndi zanu. Ndinu mphungu. Ndicho Chakudya chanu.

²⁴⁰ Iye ankadziwa kuti, mwa mphamvu ya Mulungu, Iye akanadzachita izo, chifukwa izo zinaloseredwa kuti Iye akanadzachita izo. Ndi chifukwa chake Iye sankachita mantha kunena, “Phwasulani kachisi uyu. Ine ndidzamudzutsa iye mmasiku atatu, chifukwa Davide anati, ‘Ine sindidzasiya moyo Wake mu gehena, ngakhalenso Ine sindidzalola Woyera Wanga Ameneyo kuti awone chivundi.’” Iye ankadziwa kuti palibe khungu limodzi la thupi lake likanawonongeka. Ndipo ilo limawonongeka mu maora sevente-thuu. Iye anati, “Phwasulani kachisi uyu. Ine ndidzamudzutsa iye kenanso, mmasiku atatu amenewo.” Chifukwa chiyani? Iye anali wodzaza ndi mphamvu yofulumizitsa imeneyo imene inafulumizitsa Mawu aliwonse. Iye anayang’ana mmbuyo ndipo anawawona Mawu aliwonse amene Mulungu analemba za Iye, ndipo mneneri anati Iye anakwaniritsa izo. Iye ankadziwa kuti izo zikanadzakwaniritsidwa, nazonso.

²⁴¹ Tsopano, Mawu aliwonse amene Mulungu ananena, kodi mzimu wanu unanena “ameni” kwa Iwo, Iwo akwaniritsidwa mmoyo wanu, monga wokhulupirira?

²⁴² Kodi inu mumabweza mmbuyo pa chinachake, kuti, “Chabwino, mpingo wanga umaphunzitsa mosiyana”? Ndiye usamale, khwangwala.

243 Zindikirani. Mphungu zimakhulupirira. Sipamakhala kukaikira kwa, kwa izo. Izo zimawakhulupirira Iwo. Zindikirani.

244 Tsopano, Iye ankadziwa kuti izo zikanadzachitika chifukwa Mawu anati Iwo anali. Ndipo Mawu aliwonse olembedwa za Iye ankayenera kuti adzakwaniritsidwe. Iye ankadziwa kuti Iwo analembedwa mwa mphamvu ya Mulungu, ndi aneneri ojera amene analosera kuti Iye akanadzachita zimenezo.

245 Ndipo ulosi sumalephera nkomwe. Iwo sungatero. Mawu a Mulungu sangalephere. Ndipo analembedwa mu . . . mwa Mzimu kuti . . . Ndipo tsopano, nawonso, Mzimu umene unamuukitsa Yesu kwa akufa, ngati Iwo ukhala mu umunthu wanu, thupi lanu, Iwo udzafulumizitsanso thupi lanu lachivundi. Ndiye, liwombereni ilo, liwotcheni ilo, chitani chirichonse chimene inu mukufuna kuchita, lisekeni ilo, liphwanyeni ilo, likaneni ilo, chitani chimene inu mukufuna kuchita. Mulungu adzalidzutsa ilo, pakuti Iye anati Iye adzatero. Ndipo woyera aliyense wa Mulungu ali ndi lonjezo limenelo mwa iye, amadziwa kuti icho ndi Choonadi. Chotero, musawope, m'bale, ife tiri kale mu Isitara.

246 Tayang'anani tsopano pa chiwalitsiro, ife tisanatseke. Chiwalitsiro, chiwalitsiro, ife tonse tikuumiridwa pamenepo mu chiwalitsiro. Taonani zimene tikuziwona lero. Zindikirani basi zimene ife tikuziwona lero, mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu. Ife tonse tinali kumeneko. Uko kunali ojera akufa, akuyimiridwa mwa Mose; apo panali chiwukitsiro; ndi Yesu Khristu waulemelo. Elisha . . . Mose, Eliya, ndi Yesu, onse atayima pa phiri; ojera akufa, ojera okwatulidwa; ndi Yesu waulemelo. Oh, mai!

247 Chabwino, inu mukuti . . . Ine ndinamumva mnyamata akunena. Iwo adzati, "Anthu inu, bwanji, ngati inu mukanakhala ndi mphamvu ya mtundu uwu, inu mumayenera kupita uko ndi kukawauza anthu chimene inu mungachite." Zikhale kutali ndi Mkhristu weniweni, kunena chinthu chonga chimenecho. Mukuona? Ndithudi, ife sitidzinenera mphamvu ayi. Ku . . .

248 Koma ife timachita chinthu chimodzi. Pamene iwo anyang'ana pozungulira, ndi mphamvu zonsezi pa iwo, "Anawona Yesu yekha." Ndipo wokhulupirira weniweni, woona samasamala kaya iye akuikira kumbuyo chipembedzo, kapena palibe kanthu za icho. Iye amangofuna chinthu chimodzi chokha, kuti inu mumuwone Khristu waulemelo ameneyo, zimapanga kusiyana kulikonse. Chenicheni, chochitika choona cha Phiri la Chiwalitsiro chimangolemekeza Yesu Khristu yekha. Icho sichinamulemekeze Mose, sichinamulemekeze Eliya, sanadzilemekeze iwoeni, sanalemekeze china chirichonse, koma iwo anamuwona Khristu waulemelo. Ndipo wokhulupirira

woona aliyense, icho ndi chimene chiri mu mtima mwake, kuti azilemekeza Yesu Khristu. Ndicho chimene iye akuyesetsa kuti anthu achiwone.

²⁴⁹ Osati kunena kuti, “Chabwino, ngati inu mubwera kudzajowina magulu athu, ngati inu mubwera kudzapanga *ichi* kapena *icho*.” Oh, musachite zimenezo. Musachite zimenezo.

²⁵⁰ Onani Mawu a Mulungu, amene ali Khristu, akukulitsidwa; ndi kukwaniritsa lonjezo la tsiku lino, mu ora lalikulu ili la chiwukitsiro. Zindikirani. Ndipo zimawapatsa iwo chisangalalo, kudziwa kuti ife tiri ndi Iye, mnofu wa mnofu Wake, ndi fupa la mafupa Ake. Ndi chisangalalo bwanji! Ndicho chinthu chokhacho chimene wokhulupirira weniweni amasamala nacho.

²⁵¹ Iwo samasamala za chipembedzo. Iwo samasamala za bungwe. Iwo sasamala chimene akazi ena amaganiza. Iwo samasamala. Ndithudi ayi. Iwo sadzachita zinthu izi zimene a...akazi enawa amachita. Iwo...Amuna awa sangachite zinthu zimenezo. Iwo sangakhale ndi kumasasatitsana ndi bungwe lina, kupewa kutulutsidwa, ndi kuwopa kuti sapeza tikiti ya chakudya. Iwo samasamala za zinthu zimenezo. Ndi zamkutu kwa iwo.

²⁵² Pali chokhumba cha mtima chimodzi chokha, ndicho, kumuwona Yesu Khristu akulemekezedwa. Khalidwe lawo likuyenera kukhala ndi Mulungu. Ilo likuyenera mwamtheradi, kukhala osati china chirichonse, koma ulemelero wa Yesu Khristu wokha. Ndipo kodi Yesu ndi chiyani? Mawu. Nkulondola uko? Tsopano, zindikirani, ndi kuwona njira Yake yotsimikizidwa yomweyo, ikutsimikizira chiwukitsiro Chake. Tsopano icho ndi chiyani? Kuwuwona moyo wanu, mwa Mawu Ake olonjezedwa amene Iye anati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse,” kutsimikizira kuti Iye akanali moyo.

²⁵³ Ine sindikusamala ngati khomo lililonse mdzikoli latsekedwa kwa ine. Kuti, ine ndi...Monga ine ndinanenera, ine ndinali fifite-sikisi, tsiku lina. Ine ndikhoza kuchotsedwapo. Ndiri pa msinkhu wa matenda a mtima. Ine ndiri mu usinkhu wina wonse uwu, ndi china chirichonse. Chabwino, ndi kusiyana kotani? Izo sizinapange kusiyana kulikonse kwa ine pamene ndinali mwana. Izo sizikupanga kusiyana kulikonse tsopano, ora limene nambala yanga idzaitanidwe, ndi khadi langa kuchokera pa alumali. Ine sindikusamala ngati iwo ankadziwa konse kuti ine ndinakhalapo pa dziko lapansi. Izo sizimandipanga ine wosiyana. Iwo sakuyenera kukhala ndi zoyimikidwa zazikulu ndi nyumba zazikulu kuti azinena kuti ndinali kuno padziko lapansi.

²⁵⁴ Chinthu chimodzi chokha chimene ine ndikufuna kuti iwo adziwe, kuti adziwe kuti “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ndipo mu mtima mwanga ine ndagwira mtheradi Wake. Ndipo ine ndikudziwa kuti

tsiku lina. . . Ngakhale, ine ndikhoza kumizidwa mu nyanja. Ndikhoza kukaphedwa ku Afrika. Sindikudziwa chimene chiti chidzandichitikire ine. Koma chinthu chimodzi chimene ine ndikuchidziwa, ine ndiri ndi mtheradi. Aleluya! Khomo lililonse likhoza kutsekedwa. Izo sizikupanga kusiyana pang'ono kwa ine. Ine sindikuyesera kulemekeza munthu wina kapena bungwe lina, ngakhale inemwini, kapena palibe gulu lililonse, kapena palibe china chirichonse. Ine ndikufuna kuti anthu amuwone Yesu Khristu akuwukitsidwa kwa akufa, ndipo Mzimu Wake ukukhala moyo. “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

²⁵⁵ Nzosadabwitsa, Yesu anati, “Musawope. Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, koma ndiri wamoyo kwanthawizonse.”

²⁵⁶ “Pakuti tsopano ife tawomboledwa ndi Iye, ndipo tawukitsidwa ndi Iye, ndipo tsopano (osati tidzakhala) tikukhala mmalo Ammwambamwamba mwa Iye.” Tsopano, pamene ife tiri ndi Mzimu uwu mwa ife, mtheradi, zimawonetsera kuti zokaikira zonse zachotsedwapo. Chiyani? Khristu akukhala moyo. Osati *ine* ndikukhala moyo; osati *ine*. “Khristu akukhala moyo mwa ine.” Osati *inu* mukukhala moyo, koma Khristu akukhala moyo mwa inu; chifukwa Mawu Ake amoyo akukhala mwa inu, kusonyeza kuti nkhani zonse za Amethodisti anu onse, ndi Abaptisti, ndi malingaliro Achipentekoste, china chirichonse, zinachotsedwapo. Ndipo Yesu Khristu. . .

²⁵⁷ Monga pa Phiri la Chiwalitsiro, aneneri onse ndi china chirichonse chinatsirizika. Masiku onse a Chilutera, Methodisti, Presbateria, onse ali bwino, koma, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa. Mvereni inu Iye,” Mawu a ora lino, ora la Zisindikizo. Pamene, zinsinsi zonse mmbuyo kutaliko, zimene zakhala zitabisidwa zaka zonsezi, ndipo izo ziri. . . Piramidi yaikulu ija ya nthawi ija inachotsedwapo, mwala wapamutu, kuzipanga izo mwanguli kuti Nyenyezi ya Davide idzakhazikike mmalo Ake. Ndipo Mpingo waukulu wa Mulungu wamoyo udzaukitsidwe monga mapiko a mphungu, utanyamulidwira uko ku Ulemelero. Inde.

²⁵⁸ Mu tsopano, mu tsopano, mmatupi athu: ndi kuyankhula ndi malirime atsopano; ndi kunenera, ndi kuwoneratu; kuika manja pa odwala, ndipo iwo nkumachira; dziko, lakufa, ndi zinthu zonse za mdziko. Ife tadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, ndipo ife tsopano tagwirizira mphamvu. Aleluya!

Pa mmawa wa chiwukitsiro uja,
Pamene zisindikizo za imfa zidzathyoledwa,
Tidzauka, (Aleluya!) tidzauka. (Ameni!)

²⁵⁹ Mulibe ziwanda zokwanira mu gehena zotilepheretsa ife kuchita izo. Ife tinakonzedweratu ndi Mulungu kwa ora lino. Mawu a Mulungu amadziwonetsera Okha kupyolera mwa ife. Ndipo ife tikukhala mu Kukhalapo kwa Mulungu, mwa Mawu

a lonjezo la Mulungu. Kulibeko mdierekezi mu gehena amene angandiletse ine kuwuka. Palibe chitseko chimene iye angatseke pa nkhope yanga, mmawa umenewo. Zisindikizo zamatulidwa. Aleluya!

²⁶⁰ Ndine mfulu. Ndine mphungu. Sindilinso mu khola, koma ndine mfulu. Ine ndauka kwa akufa, ndalowa mu Moyo watsopano wa Yesu Khristu. Osati ine ndekha, koma mwamuna aliyense, akazi, mnyamata kapena mtsikana amene wakhala pano, amene wadzazidwa mu Mzimu wa Mulungu umenewo, ndi cholengedwa chatsopano mwa Khristu. Ndipo inu ndi mphungu.

²⁶¹ Ife tiri amoyo, lero, ndipo tikusangalala ndi chiwukitsiro kwamuyaya. Chifukwa Iye ali moyo, ife tiri moyo, nafenso. Ndipo Iye akukhala moyo ife, kutipanga ife amoyo. Ndipo Mzimu umene unamuukitsa Iye kwa akufa, wokhala mu thupi lathu, udzafulumizitsa matupi athu akufa, pa Isitara Yamuyaya yayikulu imeneyo. Ulemelero kwa Mulungu!

²⁶² Oh, tengani dziko, tengani chirichonse chimene inu mukufuna, koma ndipatseni ine Yesu. Amen. Ine ndimankonda Iye. Iye ndi dziko lonse, kwa ine.

²⁶³ Ndipo chifukwa chakuti inu ndi gawo la Iye, ine ndi gawo la inu, ndipo inu ndi gawo la ine. Ndipo, palimodzi, ndife gawo la Iye.

²⁶⁴ Oh, Mkhristu, ndi mwayi wotani umene ife tiri nawo! Ife tiri ndi mwayi umene Paulo Woyera sanalote atakhala nawo. Ife tiri ndi mwayi umene Enoki, ndi Eliya, ndi onsewo sanakhalepo nawo. Mwayi umene ife tiri nawo tsopano!

²⁶⁵ Ndipo ilipo nkhosa imodzi yaing'ono kutali kwinakwake, ndipo Iye sadzakhutitsidwa mpaka iyo itabwera mu khola. Mwa thandizo la Mulungu, ndi mwa masomphenya, ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, ine ndikubwerera kuwoloka nyanja. Nkhosa yaying'ono yotsiriza imeneyo ikhoza kukhala yakuda kumusi uko, mwa zonse zimene ine ndikudziwa, kumene iwo samaganiza nkomwe kuti iwo ali ndi solo. Koma Mulungu amadziwa mosiyana. Ine ndikafunafuna mpaka tsiku lotsiriza la moyo wanga, kuti ndikaipeze imeneyo, kulikonse kumene iyo ili.

²⁶⁶ Ndikuyembekeza kuti sindinakhumudwitse aliyense wa abale anga ponena zinthu zokhwima izi. Ine... Osati kuti sindikufuna kuti muzipita ku tchalitchi. Ndithudi, ine ndikufuna kuti inu muzipita ku tchalitchi. Inu muzipita ku tchalitchi kulikonse kumene inu mukupita. Koma musalole icho chikhale chiyembekezo chanu, kunena, "Chabwino, ine ndine wa *ichi*, kapena ine ndi wa *icho*." Oh, m'bale, mlongo, mukhale wa Khristu. Zipitani ku tchalitchi, koma mukhale wa Khristu. Amen.

²⁶⁷ Mulole uko—mulole kugwirizitsa uko, ngati iko sikuli mwa inu, kukufulumizitsireni inu pakali pano ku Moyo. Kodi inu simulandira Iwo tsopano?

268 Chipinda ichi chadzaza ndi Iwo. Ine ndikumverera Iwoponse pondizungulira ine. Ine ndikudziwa Iwo uli pano, mphamvu ya Mulungu, Woonawamkulu wa masomphenya, Woneneratu wamkulu amene akhoza kunena zinthu ndipo izo nkusalephera, Mmodzi wamkuluyo amene akhoza kuyankhula ndipo palibe munthu anganene kuti “ayi,” Munthuyo akhoza kutsegula ndipo palibe munthu angatseke. Iye amene anali wakufa ali moyo tsopano, ndipo wamoyo, lero, kuno mu Phoenix, akuyenda pakati pa maluwabwamba obadwa kumenewa.

269 Nzosadabwitsa, mmawa wa Isitara umenewo madontho ang’onoang’ono a misozi ya mame anali pa tsamba lililonse la kakombo ndi duwa lililonse. Chifukwa chiyani? Ilo linadziwa kuti ilo linadutsitsidwa kupyola mu nthaka, ndipo penapake pali duwa Lamuyaya likuphuka. Ilo lidzatenga malo ake tsiku lina. Uko nkulondola.

270 Nzosadabwitsa, misozi yachisangalalo imatsika mmasaya athu. Nzosadabwitsa, mitima yathu imagwendera ndi kunjenjemera pamene timverera mphamvu yosintha yomweyo ikubwera mmiyoyo yathu ndi kutidzaza ife, ngakhale potilola ife kuyankhula mu chinenero chochokera Kumwamba.

271 Ife tafulumizitsidwa kufika mu Kukhalapo Kwake pamenepo, kulosera, kuwoneratu, kuneneratu, ndi chirichonse chikugunda mwangwiro ndi Mawu. Ngati izo zikunenera mosiyana ndi Izo, musazikhulupirire izo. Koma ngati izo ziri ndi Mawu, Iwo ananenedwa kale, PAKUTI ATERO AMBUYE.

272 “Musawope ayi. Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, ndipo wamoyo kwanthawizonse.” Chimenecho ndi chisindikizo cha Isitara cha Mulungu chimene chimasindikiza chirembo chirichonse cha Mawu awa mu mtima mwanu. Kodi chisindikizo ndi chiyani? “Inu ndi akalata olembedwa, owerengedwa ndi anthu onse.” Inu mukudziwa zimenezo. Koma pamene Mulungu anakutangani inu, Iye anakusindikizani inu ndi chisindikizo cha Isitara, kuti mwaukitsidwa ndi Khristu, ndipo ndinu cholengedwa chatsopano.

273 Ngati inu simunasindikizidwe mmawa uno, chitani chomwecho pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

274 [M’bale akuyamba kuyankhula mu lirime lina. Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . Ambuye. Inu mukumva zimenezo?

275 Talingalirani tsopano, ndi mitu yanu yoweramitsidwa. Aroma 8:11, “Ngati zingakhale kuti Mzimu umene unamuwukitsa Khristu kwa akufa ukukhala mwa inu, Iwo udzafulumizitsanso matupi anu achivundi.”

276 Kodi ife tingamayembekezere chiyani, anthu? Chatsala ndi chiyani pamenepo? Tayang’anani pa Formosa ndi dziko lonse lapansi. Ndipo mabomba a atomiki ndi china chirichonse zakonzeka kuti zikanthe dziko, ndipo ndi amanjenje ochuluka, ndi mantha, ndipo akukuwa. Ndipo zotsanzira za kanema izi

zikuchitika, kunja uko, kumangonena nthabwala zamtundu uliwonse, monga ngati mnyamata wamng'ono akudutsa pamanda, akuyimba mluzu usiku, kuyesera kuwapangitsa anthu kukhulupirira kuti chirichonse chiri bwino. Inu musanyengedwe. Kudza kwa Ambuye kuli pafupi.

²⁷⁷ Inu munazindikira, tsiku lina, nsodzi anabwera ndipo anadzandiuza ine, nditakhala pansi kutsidya pa gombe, kuti, mtundu wina wa nsonga yophwasuka kapena chinachake kumusi kuno. Ndipo momwe, kuti, kalekale chivomezi chija chisanagwedeze mu Greece, nsomba zonse zimene kawirikawiri zimadya pafupifupi nthawi imeneyo ya mmawa, izo sizinadye. Chinali chiyani icho? Izo sizinali pamwamba. Nthawi yachiwiri icho chinachitika, chinthu chomwecho chinachitika. Iye anadziwa pomwepo kuti chinachake chichitika. Nsomba zimenezo sizinkadya pa nthawi imeneyo.

²⁷⁸ Ndipo mbalame zonse ndi zinthu zimene zimadya nsomba, izo zinasiya kudya. Kulawirira kumeneko m'mawa, ndi pamene izo zimadya. Izo zimangokhala mmbali mwa gombe, zimachoka ku mphanga ndi zinthu. Pakuti, mu maminiti pang'ono okha, ndere za mnyanja zimayamba kuwira kuchokera mu nthaka, kuchokera pansi pa nyanja. Mukuona? Nsomba zimenezo zimadziwa izo zisanachitike.

²⁷⁹ Ndikupita ku India, ndinawerenga pepala, linati, "Chivomezi chiyenera kuti chatha." Kwa masiku, mbalame zazing'ono sizinkabwerera ku zisa zawo mmathanthwe. Ng'ombe sizimayima mozungulira malo obisalamo pansi pa . . . mu mthunzi, pa kutentha kwa tsiku. Nkhosa zinaima pakati pa munda, zinatsamirana ina ndi imzake. Izo sizimapita kumtunda kuzungulira miyala imeneyo, masiku awiri kapena atatu chivomezi chisanachitike.

²⁸⁰ Chifukwa chiyani? Nkhosa zimenezo zinkadziwa izo. Izo zinkadziwa kuti chinachake chichitika. Mbalame zimenezo zinkadziwa kuti chinachake chichitika. Mbalame zammadzi zimenezo zinkadziwa kuti chinachake chichitika. Nsomba zimenezo zinkadziwa kuti chinachake chichitika. Ndi Mulungu yemweyo amene anatsogolera nyama zimenezo kulowa mu chombo.

²⁸¹ Kodi inu simukuwona, anthu odzazidwa ndi Mzimu, chinachake chikukonzekera kuti chichitike? Musayang'ane *chinachake* chachikulu chapadziko lonse chimene chikusesa; palibe koma Kudza kwa Ambuye Yesu. Kumbukirani, mungokumbukira Mawu ndi lonjezo la Ambuye.

²⁸² Kodi simubwera mofulumira? Chokaniko ku makoma aakulu amenewo. Chiwukitsiro chayandikira tsopano. Ngati pali winawake pano amene sakudziwa kuti adzapita mu chiwukitsiro chimenecho, ndipo sakutsimikiza kuti ali nayo mphamvu ya chiwukitsiro imeneyo ikukhala mwa iwo!

283 Ngakhale mphutsi zapakhungu zitawononga ilo, ngakhale bomba la atomiki litaphulika pakati panu, izo sizidzawononga konse mphamvu yofulumizitsa imeneyo, ya chiukitsiro. Ayi, ayi. Mlongo, m'bale, dzina lanu lofunika linaikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa kutali uko. Palibe munthu angalifufute ilo. Palibepo zofufutira zokwanira, mu dziko, kuti zifufute dzina lanu kulichotsa mu Bukhu Kumeneko kumene Magazi Ake anagula izo.

284 Ngati simukutsimikiza za zimenezo, musati—musatengerepo mwayi pa izo tsopano. Mukuona? Inu mutha kutenga mwayi wodutsa pa chotchinga kwinakwake ndipo osaphedwa, koma simudutsa pa chotchinga ichi. Ayi, ayi. Inu muzipeza izo. Inu simukusowa kuti mutero. Pali kwala kofiyira kukuthwanima tsopano. Lambalalani, lambalalani malingaliro anu omwe, lambalalani zinthu za mdziko.

285 Bwerani. Tiyeni tiukitsidwe limodzi mu nthawi ya Isitara yopambana iyi, chikondwerero chachikulu cha Isitara. Kodi mungakondwerere iyo mu mtima mwanu sabata ino? Ngati inu simungatero, kodi inu mungangokwezera dzanja lanu kwa Mulungu?

286 Ndikuti, “Mulungu, sindiri wotsimikiza za izo. Sindikudziwa ngati ndingathe kuchita zonsezo kapena ayi. Kodi Inu mungandithandize ine? Ine ndikwezera dzanja langa kwa Inu, Ambuye. Ndithandizeni ine.” Mulungu akudalitseni. Mulungu akudalitseni. Izo nzabwino. “Ine—ine—ine ndikufunani Inu, Ambuye. Ndithandizeni ine. Ine—ndikufuna—ine ndikufuna ndidzawukitsidwe. Ine—ndikufuna ndidzatero. Ine ndikufuna ndikhale nazo zogwirizitsa pakali pano. Ndikufuna kudziwa kuti izo ndi zolondola. Ine ndikufuna kudziwa kuti ndi zolondola, Ambuye. Ine ndikudziwa, sindingapange ku- . . .” Inu simukufuna kulakwitsa pamenepo. Izi sizikhala . . . zidzakhala mochedwa kwambiri. Tsopano ndiro tsikulo. Mai! Tsopano ndiro tsikulo. Musadikire.

287 Osati kale kwambiri, ine ndimalalikira. Uko kunali bambo wachikulire wachikuda anabwerera uko kuseri kwa nyumbayo, anakomana nane. Anati, amati, “Abusa, ndikufuna ndikuuzeni inu. Ndikunena kuti inu mukulondola.” Iye anati, “Ine ndawauza kale Ambuye, nthawi yayitali yapitayo, ine ndikufuna ndidzakhale nayo tikiti yanga mdzanja langa mmawa umenewo. Ine ndikufuna kudziwa kuti iyo yalembedwa bwino.” Anati, “Padzakhala mavuto ambiri kumusi uko pa mtsinje.” Iye anati, “Ine—ine—ine ndikutsikira kumeneko, mtsinje umenewo.” Iye anati, “Ine—ine sindikufuna mavuto kumeneko. Ndikufuna ndiziwongole zonse pomwe pano.” Izo nzoona.

288 Muli nayo visa yanu? Ngati mulibe visa yanu . . . Mukhoza kukhala ndi pasipoti, koma, ngati mulibe visa yanu,

simungalowe mu Dzikolo. Inu mukudziwa zimenezo. Kodi chanu chirichonse ndi chokonzeka? Ngati sichoncho, pakali pano ndiyo nthawi yoti muchite izo.

²⁸⁹ Musawope ayi, ngati muli ndi mantha pang'ono. Tsopano, pali pafupifupi manja handiredede anakwezedwa mmwamba muno. Chotero ngati mukungochita mantha pang'ono, tsopano tiyeni tingozikhazikitsa izo.

²⁹⁰ Tsopano, ndikudziwa kuti tiri ndi njira zosiyanasiyana. Amuna ena amati, “Bwerani, ndiloleni ine ndikugwireni chanza.” Ena amati, “Bwerani, mudzagwade pa guwa.” Tsopano, izo ndi zabwino. Ine ndiribe mawu amodzi oti ndinene motsutsa izo, nkomwe, palibe kalikonse, chirichonse chimene iwo anganene.

²⁹¹ Koma ndiloleni ine ndingokuuzani inu njira yanga. “Onse amene anakhulupirira, onse...” Kubwera ku guwa sikungakupangitseni inu kukhulupirira. Kugwirana chanza ndi mtumiki sikungakupangitseni inu kukhulupirira. Koma ngati inu mwaitanidwa ndi Mulungu, ndipo ndinu mphungu, kuyamba ndi kuyamba, kufuula kokha kumakuuzani inu. Inu mukhulupirira. Ngati inu mukukhulupirira izo kwenikweni, ine ndipemphera nanu inu.

²⁹² Kodi inu mungalingalire mphungu yaying'ono ija ikukhalabe mu khola limenelo motalika? Ayi, ayi. Huh-uh. Ayi. Usakhale pano motalika, mzanga. Tiyeni—tiyeni tikwatule tsopano. Chisomo cha Mulungu chiri pano kuti chichite zimenezo.

²⁹³ Atate Akumwamba, ife tikuzindikira kuti ife tikubwera ku ora lotsekera. Ife tiribe nthawi yayitali yokhala pano tsopano. Osati monga m'badwo wathu, koma pa nthawiyi. Ife tikukhulupirira kuti pali achinyamata ambiri amene akhala pano, adzakhala ali moyo pamene izi zizidzachitika. Izo zikhoza kuchitika lero. Sitikudziwa miniti kapena ora. Koma, Ambuye, Inu munatiuza ife, “Mukadzaona zinthu izi zikuchitika,” ndipo izo zakhala zikuchitika tsopano kwa nthawi yaitali.

²⁹⁴ Ife tikudziwa kuti nthawi yatheratu, malingana ndi asayansi. Zaka sikisi, seveni zapitazo, ife tinali maminiti atatu kuti tifike pakati pausiku. Sitikudziwa kuti ndi nthawi yochulukuka bwanji, ikugundabe, koma tikudziwa kuti tiri pamenepo.

²⁹⁵ O Mulungu, kukhala ndi chitsimikizo chimenecho: kuwona kuti mtima wathu umavomereza lonjezo lirilonse la Mulungu ndi “ameni,” kuwona kuti Mzimu Iwoweni, umene wabwera mwa ife, ukufulumizitsa umunthu wathu.

²⁹⁶ Mulungu, mulole abale anga awone zimenezo, mmawa uno. Mulole abale anga awone zimenezo, kuti Mzimu umenewo umabwera ndi kudzafulumizitsira ku Mawu. Mulole alongo anga awone chinthu chomwecho, Ambuye. Ndiyeno, ngati

iwo ati awone chinachake chimene sichingawalole iwo kufulumizitsidwira ku Mawu amenewo, O Mulungu, mulole iwo achichotse icho mwamsanga. Perekani izi, Atate. Zonsezi ziri mmanja Mwanu tsopano. Ine ndikudziwa ndalephera mu zinthu zambiri, ndipo ndikupitiriza kulephera, koma, Ambuye, ine ndachita zonse zimene ine ndikuzidziwa kuchita kwake. Tsopano izo ziri mmanja Mwanu. Iwo ndi Anu. Mu Dzina la Yesu, alandireni iwo, Atate.

²⁹⁷ Tsopano kwa inu amene muli pano ndipo amene mukusowa machiritso a thupi lanu. Ndi okhulupirira angati ali muno? Kwezani dzanja lanu. “Ndine wokhulupirira, monga momwe ndikudziwira mtima wanga.” Ndi angati omwe ali nacho? Inu mukudziwa, kupyola mthunzi wa kukayika, kuti mu mtima mwanu, pakali pano, inu mwaukitsidwa kwa akufa? Inu mukudziwa? Oh, mai! Chingachitike ndi chiyani mu msonkhano ngati uno? Ine ndikudziwa kuti ndachedwa, koma chingachitike ndi chiyani pakali pano? Tangoganizani za chimene chingachitike. Zogwirizitsazo ziri mwa inu kumene. Mukuona? Inu, ndi dzanja lanu mmwamba, mwatenga ngati—ngati lumbiriro, kwa Mulungu, kuti, “Ndikudziwa kuti chinachake chachitika kwa ine. Ine ndikhoza kusakhala pamene ine ndikuyenera kukhala.”

²⁹⁸ Inenso sindiri. Ayi, bwana. Ndiri kutali ndi pamene ndikuyenera kukhala. Koma ine ndikudziwa chinthu chimodzi ichi, ine ndadutsa kuchoka ku imfa ndapita ku Moyo. Ndikudziwa kuti chinachake chinachitika kwa ine. Ambiri... Osati ngati zambo wokalamba tsopano, koma zambiri, zaka zambiri zapitazo, izo zinachitika.

²⁹⁹ Ndipo ine ndikudziwa, tsiku limenelo pamene ine ndinalowa mu chipatala chimenecho, pamene ine ndinali ndi vuto langa lalikulu. Ine ndinamuwona mkazi wanga akufa; ine ndikuitanira moyo wake. “Ndipo ine ndachita chiyani koma kuyima pa ngodya ya msewu ndi kulalikira, ndi kupempherera odwala?”

Ndipo Satana anati, “Chabwino, Iye sangayankhe pemphero lako.”

³⁰⁰ Ine ndinamuwona iye akufa, koma ine ndikudziwa kuti mwa iye munali mphamvu ya chiwukitsiro imeneyo. Mafupa amenewo adzadzukanso.

³⁰¹ Ine ndinamuwona mwana wanga wamng’ono atagona pamenepo. Ndipo ine ndinayika dzanja langa pamenepo, ndikuti, “Mulungu, musamutenge iye.”

³⁰² Zikuwoneka ngati Iye anakokera chophimbacho pansu, anati, “Ine sindikumvanso iwe kenanso.”

³⁰³ Satana anati, “Ndi zimenezotu. Mawu amodzi okha...” Iye ankadziwa bwino kuposa kundiuza ine kuti kunalibe Mulungu, chifukwa ine ndinkadziwa zimenezo. Koma iye anati Iye samandikonda ine, Iye samasamala za ine. Mukuona?

Chifukwa chirichonse, anati, “Ndiwe mnyamata chabe, komabe usinkhu wa zaka twente. Apo pagona mkazi wako wagona muno mnyumba yosungira mitembo. Ndipo apa pali mwana wako akupita kumeneko. Ndipo—ndipo basi. . .Iwe unati Iye anali Mchiritsi wamkulu, ndipo Iye ali zonse *izi*. Ndipo, taona, kodi Iye akuchita chiyani? Mawu amodzi, Iye sangasowe ngakhale kuti awayankhule iwo, kungoyang’ana pansi apo ndi kunena. Kungogwedeza mutu Wake, ndizo zonse zimene zingachitike, ndipo iye angachiritsidwe. Koma, iwe wawona, Iye samakukonda iwe. Iye samasamala za iwe. Kulola mwana wako azifa pomwepo tsopano, ndipo ngakhale kukana kumva pemphero lako mu ora la mdima ili.”

³⁰⁴ Chirichonse chimene iye ananena chinali choona mwamtheradi. “Ndiye iwe wapanga chiyani? Kugwira ntchito tsiku lonse, mpaka osatha kuti uyimirire. Ndipo kenako kukhala tsonga usiku wonse, mpaka thwelofu ndi wani koloko. Kuyima pa ngodya za misewu, kulalikirira. Kuyimba mafoni ku chipatala. Kungobwera ndi kudzakhala pansi, pampando, kukhala pamenepo ndi kugona ora limodzi kapena awiri, ndi kubwerera ku ntchito kenanso. Usiku wotsatira, chinthu chomwecho. Ndipo ndi iwe apa, pafupifupi usinkhu wa zaka twente-wani, twente-thuu. Mzako aliyense, dona wamng’ono aliyense, mnyamata wamng’ono aliyense amene iwe unayamba wayanjanapo naye, amakutcha iwe munthu wopenga. Kodi iwe wachitapo chiyani? Iwe unadzipanga wekha kukhala chitsiru. Kodi sukuwona zimenezo?” Ine ndinangotsala pang’ono kuti ndivomerezane naye iye.

³⁰⁵ Ndipo Chinachake pansi mwa ine, imeneyo inali mphamvu yofulumizitsa ija. Ine ndinati “Ambuye anapereka, ndipo Ambuye watenga. Lidalitsike Dzina la Ambuye.”

Pamene ziyembekezo zanga zonse zatha,
Ndiye Iye ndi chiyembekezo changa chonse ndi
pokhalapo.

Pakuti pa Khristu, a . . .
[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . .
mchenga wotitimira.

Oh, Iye adzabwera ndi nkokomo
wachigonjetso,
Ndiye mulole ine mwa—mwa Iye ndidzapezeke,
Nditakutidwa mu miinjira ya chirungamo
Chake.

³⁰⁶ Osati mu chaine mwini; ine ndiribe kalikonse. Changa ndi nyansi, nsanza zakuda. Sindingakonde kuyesera kupita Kumwamba pa kulalikirira kwanga. Sindingakonde kuyesa kupita Kumwamba pa masomphenya anga. Ine ndikupita Kumwamba chifukwa ndasunga chisomo Chake mu mtima

mwanga. Chisomo chake, ndi chifukwa chake ine ndikupita. Ndi momwe tikupitira.

307 Oh, mzanga, ndiwe gawo la Thupi ili. Iwe ndi ana aang’ono a Mulungu. Tsopano, ndikunena izi kuti ndimange chiyembekezo chanu. Ngati mungapeze . . .

308 Ngati ndingapeze chisomo ndi inu, ndakuuzani inu Choonadi. . . Ndipo chimene ndakuuzani inu, ndi—ndi mneneri ananena, za zaka zapitazo. Osati kudzipanga ndekha mneneri Wake. Ayi, bwana. Koma ine ndikukuuzani inu Choonadi. Kodi Iye anayamba wanenapo chirichonse koma chimene chinali cholondola? Ine ndakudziwani inu tsopano kwa zaka twente-chakuti, kuno mu Phoenix, kuyambira nyimbo ija, *Ndikufuna Kukambirana Ndi Iye*, uko ku mpingo wa M’bale Outlaw, ine ndikukhulupirira kunali, ndi M’bale Garcia. Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye koma chimene chinadzachitika?

309 Kumbukirani, pali chiyembekezo chimodzi chokha. Pezani mphamvu yofulumizitsa iyi. Iyo idzakugwirani inu. Pamene china chirichonse chapereka njira, Iyo idzakugwirani inu.

310 Ena a iwo anati, “Kodi inu munasunga chipembedzo chanu, M’bale Branham?”

Ine ndinati, “Ayi. Icho chinandisunga ine.”

311 Icho chimandisunga ine. Ine sindimachisunga icho. Izo sikuti ngati ndikugwiritsitsa, kapena ayi. Ndi ngati Iye anagwiritsitsa, kapena ayi. Iye ndi amene anandigwiritsitsa mmalo mwanga.

312 Iye sankasowa kutero. Angelo anaikidwa mu mtengo uliwonse, anati, “Ingomasulani zala zanu. Mungoloza; simukusowa kuzichotsa izo pa mtanda. Mungoloza chala chanu, ndipo muwone chiyani.” Mwaona, gulu lonyoza lija. Koma ngati Iye akanachita zimenezo, ine sindikanakhala ndi umboni uwu lero; inu simukanakhala nawo iwo. Koma chifukwa Iye anakhala pa mtanda, Iye anagwiritsitsa pamenepo, ndi chifukwa chake ine ndikugwira ndi Iye.

Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndaima;
Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

313 Tsopano, ngati inu mukudwala, kodi inu mungayike manja anu pa wina ndi mzake. Tiyeni tipemphere. Mungoyika manja anu pa winawake pafupi ndi inu. Mosasamala chomwe chiri cholakwika ndi inu, mukhale ndi chikhulupiriro tsopano. Ngati ine ndinayamba ndakuuzanipo inu Choonadi, ine ndikuuzani inu tsopano. Mukuona? Yesu anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Ndipo ndinu okhulupirira, inu mungokweza manja anu. Musakayikire. Pali munthu wina wosauka akuvutika amene inu mwamuyika dzanja lanu. Winawake waika manja awo pa inu.

314 Kumbukirani mphamvu yofulumizitsa ija, mphamvu ija imene inamuukitsa Yesu mmanda. Tsopano inu muli ndi chikhulupiro mu chimene inu muli nacho mu lanu—mu thupi lanu lomwe. Izo zimuthandizira munthu uyo amene mwamuyikapo manja anu. “Ngati Iwo ukukhala mwa inu, Iwo udzafulumizitsanso matupi anu achivundi.”

315 Wokonedwa Mulungu, pamene ine ndaima pano mmawa uno, kuyandikira nthawi ya masana, pamene ndi pafupifupi ora ili tsiku limene Yesu anafuula, “Mulungu wanga, Mulungu wanga, ndi chifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine? Ine ndikumva ludzu.” Nzosadabwitsa, mneneri anawoneratu izo, ndipo anati, “Mafupa Anga onse, akundiayang’ana Ine. Iwo alasa manja Anga ndi mapazi Anga.” “Koma Iye anawerengedwa pamodzi ndi olakwa. Koma Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu. Iye anatunduzidwa chifukwa cha kusaeruzika kwathu. Chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tachiritsidwa.” Ife tikudzinenera izo, mmawa uno, Mulungu. Ife tikudzinenera izo.

316 Mmawa wa chiukitsiro ichi, zindikirani, Choonadi chotsimikiziridwa ichi chimene ine ndachinena, Ambuye, kuchokera mu Mawu Anu, mu Kukhalapo kwa Mulungu. Iye ndi Woweruza, ndipo ife ndi mboni kuti Iye watiwombola ife. Ndipo mwa ife muli, mwa chisomo cha Mulungu, mphamvu ya chiwukitsiro ija. Ndipo amzathu akudwala, iwo amene manja ayikidwapo.

317 O Mulungu, ife tikumutsutsa mdierekezi, pakati pa chikhulupiro chathu mmawa uno, ndi manja ataikidwa pa anthu, ndi ine ndi manja anga atatambasulira pa anthu. Mulole matenda aliwonse, kusautsika kulikonse kumene kukuyesetsa kuti kuwagwire anthu, mu kukhalapo kwa Choonadi chotsimikiziridwa ichi, zituluke. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole anthu awa akhale omasulidwa lero. Kutu, Baibulo, Mawu a Mulungu wathu anati, “Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Ndipo manja athu akhala ali mmwamba mlengalenga, kwa Inu, Mulungu.

318 Monga zomera zonse za padziko lapansi zimamwa pa kasupe Wanu, ndipo motsimikiza basi monga chomera chimenecho, chimene chaphuka, chimamwa kuchokera pa kasupe Wanu, icho chimayamba kumangidwa. Chimayamba kukula. Phesi la chimanga, duwa, chirichonse chomwe chiri chimene chikumwa mu kasupe Wanu, chimakula molunjika kwa Inu.

319 Ndipo mmawa uno, ife takula, mainchesi, Ambuye. Tikhoza kufikira pamwamba. Ife tikumwa pa kasupe Wanu. Ife ndi zolengedwa Zanu, ndi mphamvu ya chiwukitsiro mkati mwathu, Ambuye. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mumve pemphero lathu kwa abale athu ndi alongo. Ndipo mulole kusautsika kulikonse, kumene kukuwalepheretsa anthu okonedwa awa

pano amene ali ndi mphamvu iyi, Ambuye, kuwamasule iwo, kuti azitumikira Mulungu. Ndipo zikhala bwino, Ambuye. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³²⁰ Inu mukumukhulupirira Iye? Kusiya chinthu monga chonchi? Kodi mungachite bwanji izo? Inu mukungoyenera kutero, zikuwoneka ngati, mungodzokokera nokha kutali. Kodi inu mukumverera mwanjira imeneyo? Ine—ine—ine. . . Izo zikhoza kungokhala ine, kuti ine ndiri. . . Koma ine ndinali ndi kumverera, kumverera kwachirendo basi pamene ine ndibwera pakati pa anthu, pamene inu mukhala pamodzi monga chonchi. Ine ndikudziwa, kwina kwake, sizikuwoneka kuno; monga ngati wailesi, televizioni, chirichonse chimene icho chiri, chikudutsa mu chipinda chino; Khristu ali mu chipinda chino. Tangoganizani, Muomboli wathu! Tony, Iye ali pano. Amen.

³²¹ Ndipo ndani angakhale wokondwa kuposa anthu omwe ali nawo, ndi umboni wa Baibulo wa Mawu aliwonse a Mulungu akuwonetseredwa, kuti awone ngakhale kwa Angelo ndi Umunthu Wake, monga iwo achitira kudutsa a—mibadwo! Ndipo apa, Mawu a apenyi, ananeneratu ndipo izo zinachitika ndendende basi. Ndipo pano ife tiri pa kucha kwa Kudza Kwake. Oh, ndi nthawi yodabwitsa bwanji!

³²² Ife tidzamuwona Iye. Limodzi la masiku awa, Iye adzakhala pano. Mpaka Iye adzabwere, kodi inu muzindipempherera ine? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndiri ndi zovuta zowopsya patsogolo panga. Ine ndikudziwa zimenezo. Mukuona? Ndipo ine ndimakumana ndi achikunja amene akhoza kukuwombera iwe, mofanana ndi kumwa madzi, ndipo iwe nkulipidwa. Iwe umabwera pa malo awo, adierekezi amene angakutsutse iwe pa Baibulo, mophweka basi. Koma ine sindinawonepo nthawi koma chimene Mulungu wathu anapambana chigonjetso. Ine ndimapita mu Dzina Lake, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, chiyembekezo cha Moyo Wamuyaya, chiwukitsiro ndi Moyo. “Iye amene ali moyo ndi kukhulupirira mwa Ine, angakhale iye anali wakufa komabe iye adzakhala moyo. Ndipo aliyense amene akhala moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa konse.” Ine ndikukhulupirira amenewo kuti ndi Mawu Amuyaya a Mulungu. Kodi inunso mukukhulupirira momwemo? [“Ameni.”] Kodi inu mundipempherera ine? [“Ameni.”] Ine ndikupemphererani inu. Mulungu azitiyang’anira ife mpaka tidzakumanenso.

³²³ Tsopano tiyeni tiimirire pa mapazi athu, mphindi yokha. (Muli ndi chirichonse chimene mukufuna kunena?)

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

³²⁴ Sizingakhale zoyenera kuti ife tisayimbe nyimbo yaying’ono iyi, sichoncho izo? Mukukumbukira nyimbo yathu, *Ine Ndinkonda Iye*, kodi iyo ili mu mtima uliwonse? Tiyeni tingoyimba iyo. Mlongo, wokondedwa, mungatero inu. . .

Ine ndikufuna kunena kuti, ine ndikuyamikira kuyimba kwanu, inunso, mlongo. Chabwino.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

Tsopano tisintha nyimboyo.

Chikhulupiro changa chikuyang'ana kwa
Inu,
Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi Waumulungu;
Tsopano ndimvereni pamene ndikupemphera,
Oh, chotsani kulakwa kwanga konse,
Oh, ndiroleni ine kuyambira tsiku lino
Ndikhale Wanu kwathunthu!

³²⁵ Kodi izo sizikuchita chinachake kwa inu? Ndi angati amene amaikonda imeneyo mtima weniweni... Ine—ine—ine ndimakonda nyimbo za chikondwerero. Ndithudi, ine ndimatero. Koma pamene iwe ukhala mu mzimu wa kupembedza, kodi inu simumakonda nyimbo zokoma zakale izo? Ine ndikukhulupirira Mzimu Woyera unasantha pa Eddie Perronet ndi iwo amene analemba nyimbo zopambana zakale izo. Kodi inu simukukhulupirira zimenezo? Fanny Crosby, pamene iye analemba:

Msandipitirire ine, mai, O Mpulumutsi
wachifundo,
Imvani kulira kwanga;
Pamene Inu mukuitana ena,
Msandipitirire ine.

Ndinu Kasupe wachitonthozo changa chonse,
Woposa moyo kwa ine,
Ndiri ndi yani pa dziko lapansi koma Inu?
Kapena ndani Kumwamba koma Inu?

³²⁶ Kodi izo sizodabwitsa? Izo zimatipangitsa ife kufuna kuyimba *Ine Ndinkonda Iye*. Sichoncho izo? Tsopano, pamene ife tikuyimba nthawi ino, *Ine Ndinkonda Iye*, tiyeni... Ife timakondana wina ndi mzake. Ngati sitikondana wina ndi mzake, ndiye sitingamukonde Iye. Tsopano tiyeni tingogwirana chanza wina ndi mzake. Mungoimirira, ndipo mungofikira pa tebulo penapake, gwiranani chanza, wina ndi mzake.

Ine... (...?...?)
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano.

327 Ndimufunsa M'bale Williams, M'bale Williams wamng'ono, kuti abwere kuno mphindi yokha. Ine ndimufunsa iye ngati iye angawabalalitse omvetsera awa mu pemphero.

328 Ine ndimamukonda M'bale Williams, Mkhristu wachichepere, amene ine ndikuganiza kuti ndi wantchito wa Khristu moona, banja lake laling'ono. Ine ndimakhala ndi chiyanjano chochulukana ndi awa. Ndipo anyamata ofunikira a Moseley ndi onse a iwo, ife takhala tiri limodzi, ndi ochulukana a abwenzi anga okonedwa muno mu Phoenix, amene ine ndimawakonda ndi mtima wanga wonse. Ine ndikuganiza, mmawa uja mmasomphenya aja, Iye anati, "Onse amene iwe unawakondapo, ndi onse amene amakukonda iwe, Mulungu wakupatsa iwe."


329 Ndikukhulupirira winawake pano akulapa tchimo lake, panso apo, dona wamng'ono akulira.

Tiyeni tingoweramitsa mitu yathu kamphindi chifukwa cha iye.

330 Wokonedwa Mulungu, kodi iyo ndi nk'hosa yaing'ono ija imene inatsalira mu Phoenix? Ine sindikudziwa, Mulungu. Inu mukudziwa. Koma, tsiku lina, izo zidzakhala. Koma, Atate, uyu, mosakaika, ndi mmodziyo. Chotero ine ndikupemphera kuti Inu mumuthandize iye, pakali pano. Mokoma tsegulani chipata, nenani, "Bwera, mwana Wanga. Lowa kuchoka mumsewu wotopetsa, wothodwetsa. Iwe wakhala ukupunthwa kunjwa uko mu mdima. Ine ndatuluka, lero, kuti ndidzakutenge iwe. Ndi Mzimu Wanga umene ukuyankhula kwa iwe ndi kukubweretsa iwe mu khola tsopano." Perekani izi, Mulungu. Mulole mkazi wamng'ono uyu. . . basi pamphambano ya moyo kuno. "Iye amene adzamva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha." Perekani izi, wokonedwa Mulungu, kwa Mkhristu wamng'ono uyu. "Iye amene azadza kwa Ine, Ine mwanjira iliyonse sindidzamutaya konse." Pamene oyera ayimirira pa mtsikanayo, akupemphera.

331 Kumbukirani, ngakhale Paulo, amene anagendedwa moyipa kwambiri mpaka iye ankafa, ndipo pamene oyera anayima pamenepo ndipo anapemphera, moyo unabwerera. Chifukwa, mmatupi amenewo a oyera amenewo munali mphamvu yofulumizitsa ija imene inabweretsa mzimu wa moyo kubwerera kwa Paulo Woyera. Mulungu, iyo ikhoza ndithudi kupemphera pemphero, la imfa kuchoka mu. . . kapena imfa kuchoka kwa munthuyo, mwa pemphero la chikhulupiriro, ku moyo. Perekani izi, wokonedwa Mulungu.

332 Tidalitseni ife tsopano pamene ife tikuyembekezera pa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikupemphera.

333 Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, ine ndimufunsa M'bale Williams. 

65-0410 Chisindikizo Cha Isitara
Ramada Inn
Phoenix, Arizona U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org